# *Mulole Kuwala Kwanu Kuwalire Pamaso Pa Anthu*

Izi ndi zosayembekezereka kwa ine monga momwe ziriri kwa inu. Ine ndinatsikira kuno . . . Ine ndikuyenera kuvomereza kuti ndinakhala ngati ndasewera gawo la wachinyengo. Ndinabwera mochedwerapo pang'ono. Ine ndinati, "M'bale Neville akhala akulalikira pamene ine ndizifika kumeneko, chotero iye sanena mawu kwa ine. Iye azipitirira patsogolo."

2 Pamene ine ndinalowa pakhomo, Billy ananena kwa ine, iye anati, "M'bale Neville walalikira kale. Inu mwangofika mu nthawi yake."

Ine ndinati, "Chabwino."

3 Ndinalowa, iye anati, "Ine sindinayambe kulalikira panobe. Ine ndimakhala ngati ndimangodikirira."

4 Chotero ine ndinaganiza, "Chabwino, mwinamwake, ine ndikanakhoza . . . " Ine ndikudziwa iye . . . momwe zimakhalira kulalikira, kawiri kapena katatu pa tsiku, izo zimakhala ngati zimakutopetsa iwe. Ife tikudziwa zimenezo. Makamaka pamene iwo ali aang'ono monga ife tiri, inu mukudziwa, ndi anyamata aang'ono awa omwe—izo sizitenga nthawi. Chotero ife timakhala ngati limodzi, monga abale, ndipo ife timakhala ngati timagwirana mapewa athu pamodzi, ndi mitima yathu pamodzi, malingaliro athu pamodzi, kuti ife tithe kugwirira ntchito limodzi, kwa Ufumu wa Mulungu.

5 Ndipo ife timakonda kukhala limodzi ndi inu. Ndi a—ndi chinthu chachikulu. Chotero ine ndinangowapempha Ambuye kuti andipatse ine mutu waung'ono pamenepo, chinachake chimzake, kukhala ngati tiyambepo. Sindikudziwa chimene nditi ndinene panobe, koma ife tingoyamba, ndipo kenako kulikonse kumene Iye atitsogolere ife. Ndizoona kuti ife ndife . . .

6 Ine ndimayenera kuyamba msonkhano wa masiku sikisi mu Fairbanks, Alaska, fifitini, kuyambira pa fifitini. Koma sindikuganiza kuti ndingathe kufika kumeneko pa nthawi ino, chifukwa ndiri ndi kuyitanidwa kwina kumene ndikupitako, ku British Columbia. Chotero sindikuganiza kuti ndikhoza kupita nthawi ino. Ndiponso, iwo akufuna kupanga gulu la amuna amalonda, Christian Business Men.

7 Ine ndithudi ndikupempha ndi kukhumba mapemphero anu a misonkhano imene ili nkudza imene ife tikuyesera kukonzekera tsopano. Ndipo ine ndinali ndi kuyitanidwa,

masiku angapo apitawo, kwa chinachake chimene chinamveka chabwino kwa ine. Ndipo ine sindikudziwa ngati ali Ambuye mmenemo kapena ayi; ndikungoyenera kudikirira ndi kufufuza. Amuna amalonda amafuna kuti ine ndibwere ku Phoenix, mu Januware, ndi kupita ku mpingo uliwonse, usiku umodzi, monse kudutsa mu mzinda wa Phoenix, ndipo kenako nkudzakhala ndi msonkhano waukulu pambuyo pake. Izo zinamveka zosangalatsa, kwa ine, chifukwa izo zikanapereka a—mwayi kwa ine kuti ndilankhule ndi mipingo ndi atumiki onse.

8 Kawirikawiri, anthu amaganiza, pamene za ine, chifukwa ine ndimadzudzula kwambiri motsutsa mabungwe, kuti ine ndimatsutsana ndi amuna omwe ali mu bungwe. Ine sindiri zimenezo, mwa njira iliyonse. Ine ndi wa amunawo.

9 Izo ziri ngati ndimuwona munthu akubwera chotsika mtsinje apa mu ngalawa, ndipo ngalawa imeneyo inali itadzaza ndi mabowo, ndipo ine nkumadziwa izo, ndipo nkumadziwa kuti ngalawayo sikakwanitsa nkomwe kudutsa mmathithi kumusi uko. Ine ndingakhale ndikufuula ndi kumaitsutsa ngalawa imeneyo, mwamphamvu basi momwe ine ndingathere, koma osati munthu amene ali mu ngalawayo. Ine ndikutsutsa ngalawayo. Ndikudziwa kuti ngalawayo siikwanitsa izo. Ndipo ndikudziwa bungwelo silikwanitsa izo. Koma ine ndikudziwa kuti amunawo mmenemo akwanitsa, ngati inu mungatulukemo. Mukuona?

10 Koma izo ziri ngati inu munali ndi galimoto yakale ndipo mumakwera phiri, ndipo ine nkumadziwa kuti mukayamba kuseserekera mbali inayo inu mulibe mabureki. Ine sindingakhale kuti ndikutsutsana naye munthuyo, ine ndikufuula momutsutsa iye, si iyeyo, ndi galimoto imene iye alimo; iye avulazidwa.

11 Ndipo ndizo zokhudza mabungwe. Ine ndikuganiza anthu amene amagwiritsitsa ku mabungwe amenewo, ngati kuti anali Mulungu Mwiniwake, ndipo iwo amawasiya Mawu a Mulungu, basi kuti agwire bungwe. Chabwino, pamene iwo achita zimenezo, ine ndikuwopa iwo apanga kulakwitsa kwakukulu. Ndipo sikuti ndiri ndi chirichonse chotsutsana ndi munthuyo payekha, koma ndi ngalawayo imene iye wakweramo, mwaona, ine ndikutsimikiza sakwanitsa izo. Bungwe silidzakwanitsa konse kupanga izo, koma Khristu adzatero. Chotero ingotulukanimo—mu ngalawa yowukhayo ya chibungwe, mukalowe mu Chombo chotetezeka chaku Zioni, Chombo chakale chimene sichinalepherepo kuti chikafike mu nthawi, Khristu.

12 Ndipo ndizo, ndikuganiza, izo zingandipatse ine mwayi, kufika poti ndiyankhule kwa amuna amenewo.

13 Tsopano, ine ndinaganiza, mwinamwake. . .Usikuuno, ndi usiku wa mgonero. Ndipo ine ndamva kuti anali ndi ubatizo,

akhala nawo wina. Ine ndimakonda kubwera kuno ku—ku mgonero. Ine ndinasemphana nawo nthawi yapitayi, posakhala kuno. Ine ndinasemphana nawo iwo. Ndipo ine ndinadziwa kuti ili ndi Lamlungu loyamba, chotero ine ndinapanga zokonzekera kuti ndidzakhale kuno, kuti ine ndidzakhale mu mgonero wa usikuuno.

14 Pakuti moonadi ndikuganiza kuti ndi ntchito ya Mkhristu aliyense kuti azidya mgonero. Baibulo linati, "Ngati simudya iwo, inu mulibe gawo ndi Ine." Ndipo ine ndimakhulupirira kuti ndi a—nthawi yachiwonetsero kwa Akhristu. Ngati sitimadya iwo, ife sitimakhala ndi gawo ndi Iye. Ndipo ngati ife tidya iwo, mosayenera, ndiye ife tikhala olakwira Thupi ndi imfa ya Khristu. Chotero izo zimafika pa malo pamene zimamupangitsa Mkhristu kupemphera, pamene akubwera ku mgonero. Ife tiyenera kumabwera molemekeza, mwaulemu, mopatulika, kumayenda molungama, tikuvomereza zolakwitsa zathu zonse, kupempohererana wina ndi mzake. Osati zokhazo, komanso tikuyenera kumverera. . .Ngati alipo m'bale kapena mlongo pakati pathu, amene ife tikumverera kuti wachoka pa mzere pang'ono penapake, mitima yathu ikuyenera kulemedwa ndi munthu ameneyo pa usiku wa mgonero, makamaka, kuwawona iwo, kuti adzathe kuyenda akubwera ndi kudzadya mgonero, osati kutsutsidwa ndi dziko. Chifukwa, iwo ndi abale ndi alongo athu.

15 Tsopano, kwa masabata angapo apitawa, awiri kapena atatu, masabata awiri, kupita ku atatu, ine sindinalankhule mochuluka kwambiri. Ine ndakhala ndikupumula. Pakuti iyi ili ngati nthawi yanga yopumula pang'ono, ndisanakhale nako a— kukankha kwakukulu.

16 Kumumva M'bale Neville akuyankhula za zoneneratu izi pakati pa andale ndi amuna omwe ali nakodi kumvetsetsa kwa zinthu zimenezo, za nkhondo ya atomiki yomwe ili pafupi, idzayambika mu Disembara mpaka Januware. Chabwino, izo basi. . .Ndizo pafupifupi zolondola basi. Iwo alengeza izo, ndipo ayambitsa izo, ndipo kenako mabomba angapo, ndipo izo zidzakhazikitsa izo. Chotero fuko silingathe kupulumuka nkhondo ya atomiki. Ife basi sitingathe kuchita zimenezo. Koma zimenezo sizimamuwopsyeza Mkhristu, kapena sizikuyenera kumuwopsyeza Mkhristu. Ife tizikhala okonzeka pa miniti iliyonse, kuyembekezera Ambuye wathu kuti abwere. Ndipo, oh, nthawi zambiri, mwaona, izi. . .

17 Izi sizikujambulidwa, izi ndi za kwathu kuno basi. Palibe tepi, chotero sukusowa kuti uzisamalitsa zomwe ukunena, zakuti zipita kwa winawake, kapena zina zotero. Ndi anthu akwathu basi.

18 Ine ndikuuzani inu zomwe ndakhala ndikuchita. Ine ndakhala ndikupita kukasaka agologolo. Ndipo, koma, zakhala

zisakundiyendera mwabwino kwambiri. Kulibeko agologolo ambiri. Ndipo ine ndikupita ku Alaska tsopano, kukasaka nkhosa.

19 Ndipo mwinamwake anthu ena akhoza, anthu ambiri, iwe sunganene zimenezo pa tepi kapena chinachake, chifukwa pali anthu ambiri amene sakhulupirira mu zosaka, nkomwe. Ndipo, koma, nthawizonse ndimazindikira, ndi iwowo omwe sakhulupirira mu kusaka, ukangowabweretsera iwo kachidutswa ka nyama, iwo amakhutitsidwa nazo kwambiri, inu mwaona.

20 Ndipo monga donayo, nthawi ina, anandiuza ine. Iye anati, "M'bale Branham, kodi inu mukutanthauza kundiuza ine kuti—kuti mumasaka akalulu?"

21 Ine ndinati, "Inde, amayi." Tsopano, ine sindikunena za moyo wofunikawo. Iye anapita.

22 Ndipo iye anati, "Oh, zimenezo ndizamwano. Inu simukuyenera kuwombera akalulu amenewo." Chotero, kenako, sipanathe . . . Nyengoyo isanathe dona yemweyo anati, "Kodi mungandibweretsereko ine akalulu angapo?" Iye anati, "Iwo ndi tinthu tabwino kwambiri tomwe ndinayamba ndadyapo."

Ine ndinati, "Chabwino, ine ndikuganiza kuti ndi zomwe ndimadzitcha 'khalidwe.'" Mukuona?

Ndipo winawake anati, "Mukutanthauza chiyani?"

23 Ine ndinati, "Donayo ali ndi khalidwe." Ine ndinati, "Khalidwe ndi winawake amene alibe mphamvu zokwanira kupha kalulu, koma akhoza kumudya iye winawake atamupha iye. Chotero ndikuganiza kuti ndicho chimene—ndi chimene mungachitche 'khalidwe.'" Oh, ndine . . . ine sindimati . . .

24 Ndine wosamalira chirengedwe. Ine sindikhulupirira mu kupha ndi kuwononga. Ine ndimamuphunzitsa mnyamata wanga, iwo amene akusaka ndi ine, "Osatenga chirichonse pokhapokha ngati mukukonzekera kuti mukadya icho." Mukuona? Chisiyeni icho chokha. Osangowombera mbalame basi chifukwa cha chandamale. Mukuona? Kutero si bwino. Muli ndi chandamale, kakhaleni kumeneko ndipo kawombereni iyo. Inu mukadya nyamayo, ndiye, iyo inayikidwa kuno chifukwa cha cholinga chimenecho. Ndipo kuiwononga iyo, kuli ngati kuwononga china chirichonse. Sizoyenera kuchita zimenezo, kuwombera nyama ngati—ngati chandamale.

25 Ndipo pamene ine ndipita ku mapiri, abwenzi, sizimakhala mochuluka kwambiri kupita kumeneko kuti "ndikasake." Ndimapita kumeneko kuti ndikakhale ndekha ndi Mulungu. Ena a inu, ngati inu mungazindikire, chondichitikira changa chachikulu chimene ndimakhala nacho, ndi pamene ndimapita uko kokasaka, pamene ine ndimakakomana ndi Mulungu.

26 Mwa zondichitikira zanga zonse, ine sindinakhalepo ndi chimodzi monga ine ndinali nacho mmawa wina, komwe kuno, ndikupita kokasaka agologolo. Ine ndawonapo zinthu zochuluka mmoyo wanga, zizindikiro ndi zodabwitsa, ndi zina zotero. Koma icho chinandikhudza ine kwambiri kuposa chirichonse chimene ndinakhalapo nacho. Tangolingalirani tsopano, basi pafupifupi nthawi ya kucha kwa tsiku, kukugwa mvula, mitambo yokhazikika paliponse, ndikuwona utayima patsogolo panga, ukukwera mmwamba, kuchokera ngati chikho chiri pa phiri, chitakhala pamenepo, mautawaleza atatu akukwera mmwamba ndi mmwamba, mpaka iwe kuchita dzanzi paliponse mpaka kulephera kuti uyankhule. Kenako nkuyenda pafupi ndi Iwo, ndi kumumva Iye akuyankhula ndi kutsimikizira Uthenga womwewo umene iwe ukulalikira, kuti ndi Choonadi. Mukuona?

27 Anati, "Yesu wa Chipangano Chatsopano ndi Yehova wa Chakale. Iye anangosintha chophimba Chake." Chabwino, ine ndinakhala, ndikuwerenga zimenezo. Ine ndinapeza, mawu omwewo, pamene Iye "anasintha nkhope yake," mu Chigriki, ankatanthauza, "kusintha chigoba Chake." Osati kwenikweni *chophimba* Chake, koma "chigoba" Chake. Izo zinafika pa malo amene Iye "anasinthidwa," mwaona, izo zikutanthauza kuti Iye "anasintha njira Yake." Iye anali Mulungu, Yehova. Ndipo Mulungu, Yehova, anadzisintha Yekha kuchokera ku Mzimu ndipo anadzakhala Munthu. Iye ndi Yehova Mulungu yemweyo. Chimene, *uyo* anali Atate, ndipo *uyu* ndi Mwana, kukhala Munthu yemweyo.

28 Ndipo momwe, ndiye, Iye anandipatsa ine chinachake choti ndiyankhule. Ambuye akalola, ine ndikufuna kukakhala pa mtengo womwewo, mmawa, cha m'bandakucha. Ndipo ine—ine ndikuyembekeza Iye akawonekera kwa ine kachiwiri. Ine—ine ndikudalira kuti Iye adzatero, kuchitira kuti ndidziwe choti ndichite. Ndiri ndi cholemetsa mu mtima mwanga kwa anthu. Pamene ine ndikuwona ora likuyandikira ndi kudziwa kuti anthu sanakonzeke, ndipo okondedwa anga ambiri, sindikudziwa choti ndichite kapena kunena. Ndipo ine ndikupita ndi kukawona chimene Iye ati akandiwuze ine. Chotero mukhale mukundipempherera ine.

29 Ndiye ndinyamuka, mawa masana kapena Lachiwiri mmawa. M'bale kuno mu tchalitchi, ndi ine, tikunyamuka kupita ku British Columbia. Ndipo ndikupita ndi a—gulu la atumiki Achipentekoste. Izo ndizothandizidwa, ulendowo, iwo sundiwonongera ine khobidi limodzi. Ndipo iwo athandizira ulendowo ndipo anatenga namulondola. Ndipo namulondolayo ndi m'bale Wachipentekoste wodzazidwa ndi Mzimu Woyera. Ndiyeno ndiri ndi anthu ena oti ndiwabatize mu Dzina la Ambuye wathu Yesu Khristu, otchera misampha ena ndi—ndi zinthu pamene ine ndiri kumtunda uko, otchera misampha aku Norway ndi kwina kotero, amene, kupyolera mmatepi

awa amene anatuluka, awona Kuwala, ndipo akufuna kuti ine ndiwabatize iwo mu Dzina la Yesu Khristu.

30 Ndipo mkulu wa Ministerial Association of British Columbia, ine ndikakumana naye iye Loweruka likubwerali madzulo ku Pine Lodge ku Dawson Creek, British Columbia. Ndipo iye ali ndi njala ndi ludzu kuti abatizidwe mu Dzina la Yesu Khristu.

31 Chotero, inu mwaona, si kwenikweni zokasaka, abwenzi. Ine ndikufuna ndikamubatize namulondola uyu, ndi mlaliki aliyense amene akupita nane ulendo uno, mu Dzina la Yesu Khristu. Inu muzindipempherera ine. Mukuona? Chimene, ine ndikudziwa kuti ndi choonadi, chimapangitsa mtima wanga kuchitira njala ndi ludzu kuti ndimuwone Mulungu.

32 Tsopano, tisanayandikire Mawu, sinditenga nthawi yanu yochuluka, ndingophunzitsa pang'ono pokha kuchokera mu Lemba lina, mpaka ife titapeza malo, kuti tipeze pamene ife tingakhoze kupita mu kupemphera. Ndi kupeza . . .

33 Ine ndikukhulupirira winawake wayima pano. [M'bale Branham akuimikira pamene wina akuyankhula kuchokera kwa osonkhana—Mkonzi]. Ine—ine ndi, ndikhulukireni ine, kodi winawake wapafupi pang'ono anganene izo? Sindinamve chimene m'baleyo . . . [Wina akuti, "Iye akufuna kuti mumudalitse mwana wake."] Kumudalitsa mwana wake? Ndithudi, m'bale wanga. Inde, bwana. Mbweretseni mwana wanuyo. Tikhala okondwa kuchita zimenezo.

34 Ndipo, tsopano, ine—ine ndimakhulupirira mu izi. Tsopano, kuti ine ndifotokoze izo kwa anthu iwo asanabwere.

35 Kodi M'bale Arnold wabwera? Teddy? [M'bale akuti, "Inde."—Mkonzi]. Chabwino. Ngati mungatibwerere ife pa limba.

36 Tsopano, anthu ambiri amawakonkha ana aang'ono awa, ndipo iwo amautcha iwo ubatizo wa makanda. Tsopano, ngati mpingo wanu umachita zimenezo, zimenezo, izo ziri bwino. Koma, inu mwaona, ngati iwo amatero, ilo ndi dongosolo la mpingo. Ilo si Lemba. Lemba silithandizira kubatiza kwanu kuko- . . .

37 Lemba silithandizira kukonkha, mwanjira iliyonse. Palibe mmodzi anayamba wakonkhedwapo, mu Baibulo. Iwo anali, aliyense, ankabatizidwa pomizidwa mu Dzina la Yesu Khristu.

38 Koma, tsopano, makanda, mu Baibulo, iwo ankawabweretsa iwo ndipo ankawapereka iwo kwa Ambuye. Iwo ankawabweretsa ana aang'onowo ndipo nkuwadalitsira iwo kwa Ambuye, ankawapereka iwo mmikono ya Ambuye Yesu.

39 Ziri bwino, mlongo, mbweretseni mwana wanuyo. Ndipo ena aliwonsewo, amene ali ndi ana awo, amene akufuna kuti iwo adalitsidwe, bwanji, ife tikhala okondwa kuchita

zimenezo, muwupange iwo ukhale msonkhano wodalitsa ana athu aang'onowa. Tsopano, Yesu, mu Lemba, a . . .

40 Tsopano, mu tchalitchi chino kuno, ife tiri ndi mabungwe osakanikirana amitundu yonse. Ena a iwo, Achiprotestanti, ena Akatolika, ndipo ngakhale tiri ndi Ayuda amene amabwera kuno, amenewo ndi Ayuda a Orthodox. Ndi chifukwa chake ife timadzitcha tokha mosamalitsa "azipembedzo zosiyanasiyana."

41 Ndipo tsopano, kuchitira kuti inu mumvetse, ife timayesetsa, pa—pa mpingo pano, kukhala mpingo wa Malemba, basi kumangokhala ndi Baibulo. Paliponse pamene Baibulo likunena chirichonse, ife timatsatira izo ndendende mwanjira imeneyo. Tsopano, mpingo woyamba, ndipo Akhristu nonse ndi inu atumiki muvomereza kuti Iyi ndi mbiriyakale ya Mpingo woyambirira. Ife tonse tikuzidziwa zimenezo. Izi ndi ndendende zomwe zinachitika.

42 Ine ndimayankhula ndi wansembe, wansembe wa Chikatolika amakhala kuno pa msewu, posachedwapa. Ndipo iye anati, "Bambo Branham," anati, "kodi inu a—siwa Katolika kapena Protestanti?"

Ine ndinati, "Wa Protestanti."

Iye anati, "Ndiye inu mumatitsutsa ife."

43 Ine ndinati, "Ayi, bwana. Ine sindimatsutsa—sinditsutsa anthuwo, ndi—mpingo, chiphunzitso cha mpingo."

Iye anati, "Kodi inu, ndiye, kodi inu mumadzitcha nokha wa Baptisti kapena Presbateria?"

Ine ndinati, "Ayi, bwana. Mkhristu basi."

44 Ndipo iye anati, "Chabwino, mumapanga kuti mtundu wanu wa chiphunzitso? Kuti ukhale Mkhristu, umayenera kukhala ndi maziko opangira chiphunzitsocho."

Ine ndinati, "Zimenezo ndi zoona." Ine ndinati, "Ndi Baibulo."

"Chabwino," iye anati, "imeneyo ndi mbiriyakale ya mpingo wa Katolika."

Ndipo ine ndinati, "Chabwino, ndi choncho, atumwi anali akatolika?"

Iye anati, "Inde, bwana."

45 Ine ndinati, "Chabwino. Ine ndivomereza kuti izo nzolondola." Iye . . . ine ndinati, "Ndiye nanga bwanji inunso simukukhala ndi Lemba?"

46 Iye anati, "Inu mwaona, Khristu anawupatsa mpingo mphamvu yosintha Lemba nthawi iliyonse imene iwo akufuna kutero."

47 "Chabwino," ine ndinati, "ndiye inu mwasintha Ilo, ndipo mwalipatsa ilo chimene inu muli nacho lero?"

Iye anati, “Inde, bwana.”

48 Ine ndinati, “Ndiye, ine ndikufuna kuti ndifunse chinachake. Ndiye kuti Khristu ayenera kuti sakusangalatsidwa ndi Iwo, chifukwa pa Mpingo woyamba Iye anatsanulirapo Mzimu Woyera. Iwo ankachiritsa odwala, ndi kuwukitsa akufa, ndi kutulutsa ziwanda, ndipo ankachita zazikulu, zozizwitsa zamphamvu, pansi pa Chiphunzitso cha Mpingo woyamba wa katolika. Ndipo sizinawonekere mu mpingo wa Katolika kuyambira pamene iwo anasintha Chiphunzitso.”

49 Tsopano, tiyeni tibwerere ndikukhala katolika wapachiyambi. Tiyeni tibwerere mmbuyo ndi kukakhala chimene Baibulo linanena chimene iwo anali. Khristu ankayenda ndi iwo. Ndi chifukwa chake, abwenzi, chimene ife sitimayesera kuti tidzudzule mpingo uliwonse, aliwonse a anthu mmipingo, koma timayesetsa kusunga izo monga momwe Baibulo limanenera.

50 Tsopano, mu Baibulo, palibepo khanda limene linayamba labatizidwapo. Palibepo khanda limene linakonkhedwapo, paliponse mu Baibulo. Koma apa ndi pamene izo ziri mu Baibulo, linati, “Iwo anawabweretsa ana aang’ono kwa Yesu, kuti Iye akayike manja Ake pa iwo ndi kuwadalitsa iwo.” Ndipo Iye anati, “Lolani ana adze kwa Ine, ndipo musawaletse iwo, pakuti Ufumu wa Mulungu uli wa otere.” Tsopano izo nzoona ndendende. Tsopano, chotero, ife timawabweretsa ana aang’ono ndi kuwapereka iwo kuchokera mmanja mwa amayi, kapena abambo, kupita kwa Atate athu Akumwamba, ndi kuwapereka iwo mu kuwadalitsa, mu kuya konse kwa kuwona mtima.

51 Ana anga, ine ndiri nawo awiri, panobe, amene sanabatizidwe panobe, chifukwa iwo angoperekedwa kumene. Ine ndiri ndi mwana mu Ulemelero, yemwe anangodalitsidwa, osati kubatizidwa.

52 Chifukwa, ubatizo ndi wa chikhululukiro cha machimo, mwaona, kusonyeza kuti iwe walapa. Mwana ameneyo sanapange kalikonse kuti alape. Ndi mwana, wobadwa kumene kuno mdziko lapansi. Iye alibe mphamvu yoti abwere kuno, mwaona, ndipo iye alibe machimo. Pamene Khristu anafa pa Mtanda, Iye anafa kuti adzachotse tchimo la dziko lapansi. Kufikira pamene mwana uyu adzachite chinachake choti alape, Magazi a Yesu Khristu azipanga chitetezero.

53 Koma tsopano amayi ndi abambo, makolo, ali ndi ufulu womubweretsa mwanayo, ndi kumubwezera kwa Mulungu, mwana yemwe anaperekedwa kwa iwo ndi Mulungu.

54 Hana mu kachisi. Iye analonjeza. Iye anali wosabereka. Iye anali wokalamba. Iye analibe ana. Iye anapemphera moona mtima pa guwa, mpaka wansembe anatuluka ndi kukamunena iye kuti waledzera. Iye ankafuula ndi kulira, pa guwa, kuti Mulungu amupatse iye mwana. Ndipo iye anati, “Mulungu, ngati

Inu mundipatse ine mwana, ine ndidzamubweretsa iye kumalo ano ndi kudzamupereka iye kwa Inu."

55 Amayi, umo ndi momwe munapezera mwana wanu. Mulungu anakupatsani inu mwana wanu. Izo ziri monga momwe Iye anamupatsira Hana mwana wake. Ndipo tsopano inu mudzawabweretsanso ana anu usikuuno, ku kachisi, chimodzimodzi monga momwe Hana anachitira ndi Samueli wamng'ono, nayenso, mu msonkhano wowapereka. Tsopano, ife tikumudalitsa ndi kumubwezera mwana wanu, mwa pemphero, kwa Mulungu Yemwe anamupereka iye kwa inu. Ndipo ine ndikupemphera kuti anyamata ndi atsikana aang'ono awa amene ayima pano usikuuno, adzakhale aneneri ndi aneneri aakazi monga Samueli, anali wakale, kwa Ambuye, amene inu mukuwabwezera iwo.

Tsopano, ngati omvetsera angaweramitse mitu yawo mphindi yokha.

56 Mulungu wachikondi kwambiri ndi wachisomo, ife tikuyandikira mpando Wanu wachifumu wachisomo ndi chifundo, ora lino, kwa m'badwo umene ukubwera ife tikadzapita. Ana aang'ono awa amene ayima, ndipo iwo awanyamula—awanyamula iwo. Anyamulidwa, usikuuno, m'manja mwa amayi awo ndi m'manja mwa abambo awo. Iwo ndi mbewu ya mtundu wa mawa. Kuti atsimikize kuti ayamba bwino, amayi ndi abambo awa akubweretsa ana aang'ono awa kuno kuti adalitsidwe, kuti adzaipereke miyoyo yawo yaing'ono kwa Mulungu wamoyo.

57 Atate, abusa ndi ine tikupita patsogolo apa, ndi kukawapereka ana awa kwa Inu mu pemphero la kuwadalitsa. Adalitseni iwo, Atate athu. Ife tikupemphera kuti Inu muwadalitse iwo, kuti akhale antchito Anu aang'ono. Mulole iwo akhale miyoyo yaitali, yokondwa kuno pa dziko lapansi, ndi kudzawona Kudza kwa Ambuye Yesu. Osati zokhazo, mulole iwo akhale moyo wautali, wathanzi, wokondwa, ndi kukhala antchito Anu. Mulole Inu muwatsogolere iwo. Mulole Inu mukapange alaliki, oyimba, avangeri, amishonare, a mawa, kuchokera mwa ana awa, ngati kuli mawa loti libwere. Perekani izi, Ambuye. Ife tiwadalitsira iwo kwa Inu mopambana momwe ife tikudziwira, molingana ndi Lemba Lanu limene Inu mwatisiyira ife, Mawu Oyera.

58 Limene, linalembedwa mu Bukhu lotsiriza la Baibulo, "Mulungu adzachotsa mu Bukhu la Moyo, munthu uyo amene ati adzachotse Mawu amodzi a Ilo, kapena kuwonjezera mawu amodzi kwa Ilo." Ife tikuzindikira, ndiye, kuti Baibulo ndi Mawu opatulika a Mulungu. Ndipo ife sitingathe kuwonjezera chinthu chimodzi kwa Ilo, kapena kuchotsa chinthu chimodzi kwa Ilo. Chotero, Ambuye, ife tikulisiya Ilo basi momwe Inu

munaliperekera Ilo kwa ife, ndi kuliphunzitsa Ilo, ndi kuyesetsa kulikhala moyo Ilo, mwa chisomo Chanu.

59 Pamene, tikuwapereka ana awa, monga momwe iwo anawabweretsa iwo kwa Yesu mmasiku apitawo. Ngati Iye akanakhala pano pa dziko lapansi usikuuno, mmawonekedwe athupi, amayi awa ndi abambo akanathamangira pa mapazi Ake, ndi kuwabweretsa aang'ono amenewo. Ndipo Iye akanadzayika manja Ake pa iwo ndi kuwadalitsa iwo. Inu mwakhala pa dzanja lamanja la ulemelero Mmwamba, usikuuno, Ambuye Yesu. Ndipo ife tatsalira kuno, ngati wantchito Wanu. Ife tiyika manja athu pa iwo, mu pemphero kwa Inu, kuti Inu mutenge miyoyo yawo yaing'onoyo ndi kuigwiritsa ntchito iyo kwa ulemelero Wanu. Mu Dzina la Yesu Khristu, ife tikupempha izi. Ameni.

(*Abweretseni Iwo*.)

60 Inu muli ndi wamng'ono? Dzina lake ndi ndani? John. Dzina lomaliza, mlongo? [Amayi akuti, "Meyer."—Mkonzi]. Meyer. Oh! Uyu ndi John Meyer wamng'ono, wamng'ono amene ife tonse tinamupempherera, tsiku lina. Ndi uyu apa, ali ndi ife, usikuuno.

Tiyeni tiweramitse mutu wathu.

61 Ambuye Yesu, pamene m'busa Wanu ndi ine tayima limodzi mu Dzina Lanu, kutenga kuchokera mmanja mwa amayi awa, mwana wakhanda uyu, ndi abambo amene akuwonerera. Ndi ziyembekezo zazikulu za wamng'ono uyu, mmasiku ali nkudza. Ine tsopano ndikumupereka John Meyer wamng'ono uyu kwa Inu, Ambuye, kwa utumiki Wanu. Mu Dzina la Yesu Khristu, ife tikumupereka iye kwa Mulungu. Ameni.

62 Mulungu akudalitseni inu. Mulungu adalitse wamng'onoyo. Amusunge iye wokondwa, akhale a . . .?. . .

63 Pamapeto, iye anafika. Ine ndikuganiza inu munali ndi mwanayo kawiri kapena katatu, koma ine sindimadziwa izo. Dzina lake ndi ndani? [Amayi akuti, "Elisabeth Collins."—Mkonzi]. Elisabeth Collins. Chabwino. Ine ndikumudziwa iye; iye amugwetsa iye. Ndikudziwa zimenezo. Mukuona? Koma Elisabeth Collins wamng'ono.

Tiweramitse mitu yathu.

64 Atate Akumwamba, mupangeni uyu Hana wina wamng'ono. Mupangeni iye akhale mtumiki wa Ambuye. Mudalitseni iye. Adalitseni abambo ake ndi amake, mu yawo—mnyumba mwawo. Ndipo mulole iye akhale moyo kwa ulemelero wa Mulungu. Perekani izi, Ambuye. Ife tikumupereka kwa Inu, Elisabeth Collins, mu kudalitsa kwa moyo wake. Mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

Mulungu akudalitseni inu.

65 Ndikudabwa ngati mungakwezedwe pa nsanja? Ndinu? Dzina lake ndi ndani? [Amayi akuti, "Davonna Gayle Stayton."—

Mkonzi]. Davonna Gayle [“Stayton.”] Stayton. Ndi choncho. Davonna Gayle.

66 Uyu ndi Davonna Gayle Stayton wamng’ono. Amayi ake ndi iwo akhala akubwera mu tchalitchi, akhala ali . . . analandira Mzimu Woyera, anabatizidwa.

Tiyeni tiweramitse mutu wathu.

67 Athu Atate Akumwamba, ife tikusilira kulimba mtima kwa amayi awa ndi abambo achichepere, kubwera kwake, momwe iye wachitira, ndi kupita patsogolo komwe iye wapanga. Momwe Inu mwadalitsira mitima yofewa yachichepere iyi. Ife tikupereka kwa Inu wokondedwa wamng’ono uyu, kuti Inu mudalitse moyo wake waung’ono, Ambuye. Ndipo mulole iye akhale wantchito Wanu. Adalitseni abambo ake ndi amake, pamodzi. Mulole iye nthawizonse azileredwa mu nyumba ya Chikhristu, pansi pa malangizo a Mulungu. Ife tikumupereka iye kwa Inu, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

68 Mulungu akudalitse iwe, Davonna Stayton wamng’ono. Mulungu akudalitseni inu, M’bale Stayton.

69 Uli bwanji, wokoma wamng’ono? Iwe wabwera kuno, miniti yokha? Huh? Kodi ine . . . Iye akhoza kuyima pomwe pano, ngati iye akufuna kutero. Dzina lake ndi ndani, m’bale? [M’baleyo akuti, “Hannah.”—Mkonzi]. M’bale Creech . . . Khalani wamng’ono . . . Eya. Ndiwe Allen wamng’ono. Woyankhula bwino kwambiri, mwaona. Chabwino, uyu—uyu ndi Hannah Creech wamng’ono. Mwinamwake iye andilola ine kuti ndimunyamulire iye mmwamba. Iye ndi mtsikana wamng’ono wokoma.

Tiyeni tiweramitse mutu wathu.

70 Atate Akumwamba, ife tikumpereka kwa Inu mwana wamng’ono uyu, tsopano pa mapazi a amayi ake. Ndipo ife tikupemphera, Atate Akumwamba, kuti Inu mumudalitse iye ndi kuwupanga moyo wake wothandizira mu Ufumu Wanu. Adalitseni abambo ake ndi amake. Mulole mwanayu aleredwe mnyumba ya Chikhristu, malangizo a Mulungu. Tikuika manja athu pa iye ndi kumudalitsira iye kwa Inu, moyo wake waung’ono, ku utumiki kwa Inu. Mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

Akudalitseni inu, mmawa uno. Akudalitseni inu!

71 Kodi iye sakubwera? Dzina lake ndi ndani? Chiyani? Don? [M’baleyo akuti, “Don . . . ? . . . Benjamin.”—Mkonzi]. Benjamin. Benjamin. [“Kulondola. Benjamin wamng’ono.”] Uyu ndi Benjamin . . . ? . . . [“Uko nkulondola.”] M’bale wamng’ono ndi mlongo.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

72 Atate Athu Akumwamba, pamene ife tikupereka kwa Inu wokondedwa wamng’ono uyu, komabe wamng’ono kwambiri,

Ambuye, kuti adziwe chimene chikuchitika. Koma Inu mukudziwa zinthu zonse. Ife tikupemphera kuti Inu mudalitse moyo wake waung'ono, Ambuye. Mudalitse nyumba yake. Ndipo, Ambuye, mulole mnyamata wamng'ono uyu akakhale moyo kwa ulemelero wa Mulungu, wabwino, moyo wautali wokondwa; ngati nkotheka, adzawone Kudza kwa Ambuye Yesu. Perekani izi, Ambuye. Ife tikumupereka iye kwa Inu, kwa utumiki Wanu, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

73 Ndipo ameneyo anali a . . . [Winawake akuti, "Mnyamata."—Mkonzi]. Ameneyo ndi mnyamata wamng'ono wokoma. Mukuona? Benjamin . . .?. . . Mai, ndi mnyamata wamkulu bwanji uyu ali! Mai! . . .?. . . Oh, mai!

74 Ine ndimamuyang'ana wamng'onoyo, akundiyang'anitsitsa ine kwambiri. Ine ndakhala ndikumunyamula iye. Mukuona? Dzina? [Abambo akuti, "William Davis."—Mkonzi.] . . .?. . . William Davis wamng'ono. Ndithudi mnyamata wamng'ono wokondedwa, kulondola, kwa mnyamata wamng'onoyu.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

75 Ambuye Yesu, ife tikupereka kwa Inu, mnyamata wamng'ono wokondedwa, ku utumiki Wanu. Amake ndi abambo akumubweretsa iye, Ambuye, kuti iye akhoze kugwiritsidwa ntchito kwa ulemelero wa Mulungu. Tsopano, chotero, Ambuye, powerenga kuchokera mmasiku apitawo, Iye anayika manja Ake pa tiana tating'ono monga chonchi ndipo anawadalitsa iwo. Manja athu ndi oyimira osayenera a Ake. Koma ife tikupempha mu Dzina Lake, ndi kumupereka mwana uyu kwa Inu, kwa moyo wa utumiki, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

Akudalitseni inu!

76 Akazi a Bowers . . .?. . . Pano, wokondedwa, dzina lako ndi ndani? Oh, mai! [Winawake akuti, "Sussie. Sussie . . .?. . . "—Mkonzi]. Ine ndikhala wokondwa kukunyamula iwe. Ndiwe mnyamata wamng'ono wabwino. Sussie Bate wamng'ono.

Tiyeni tiweramitse mitu yathu.

77 Atate Akumwamba, mtsikana wamng'ono wa maso owala uyu . . .?. . . Osadziwa chimene chiri kutsogolo kwa msewu; palibe aliyense wa ife amene amadziwa. Koma, abambo ndi amayi, iwo akufuna kuti iye akhale mu njira yowongoka ndi yopapatiza. Ndi chipangizo chaching'ono chokongola monga ichi, momwe Satana angafunire kuti apange phokoso. Koma iwo amubweretsa iye, kuti Satana athamangitsidwe kwa iye. Ubiseni moyo wake waung'ono, Ambuye, ku utumiki Wanu. Mu Dzina la Yesu Khristu ife tikupempha izi. Ameni.

Mulungu akudalitse iwe, mtsikana wamng'ono! . . .?. . . Chabwino.

Abweretseni iwo, abweretseni iwo,

Abweretseni iwo kuchokera ku minda ya tchimo;
Abweretseni iwo, abweretseni iwo,
Abweretseni aang'onowo kwa Yesu.

78 Oh, bwanji. . . Kodi inu simumawakonda ana aang'ono? Ngati anthu samawakonda ana aang'ono, pali chinachake cholakwika. Yesu anati, "Pokhapokha inu mutatembenuka ndi kukhala monga mmodzi wa aang'ono awa, inu simudzalowa mu Ufumu." Palibe aliyense.

79 Bambo ali ndi atsikana aang'ono awiri kumbuyo uko, komabe, iye amafuna kuwabweretsa. Ndinamuuza iye, "Abweretse iwo patsogolo." Mukuona?

80 "Pokhapokha ife titatembenuka ndi kukhala monga ana aang'ono awa." Inu mukudziwa chiyani? Inu mukhoza kupweteka kumverera kwawo kwakung'ono. Abambo ndi amayi amadziwa, nthawi zambiri akalowa mu vuto, amawakwapula iwo. Bwanji, maminiti awiri, mikono yawo yaing'ono imakhala itakukumbatira iwe, ndipo amaiwala zonse za izo. Ndipo umo ndi momwe ife tikuyenera kumachitira. Ziribe kanthu zomwe zachitika, ife tikuyenera kukhala okhululukira ndi okoma mtima, kwa wina ndi mzake, ndi—ndi—ndi kukhala monga chomwecho, monga ana aang'ono, ololera ku—kukhululuka ndi kuiwala, ndi—ndi monga chomwecho. Ndicho chimene ife tiri—ife tikuyenera kumatero. Ndiyeno pamene tichita monga choncho, ife tikuyandikira ku Ufumu wa Mulungu pamenepo.

81 Ine ndikukhulupirira atsikana aang'ono awiri ali ngati amanyazi. Abambo ndi amayi akuyenera kuyenda nawo. Chabwino, izo ndi zabwino kwambiri. Ife timangozikonda zimenezo. Ife timakonda atsikana ochita manyazi. Si kawirikawiri kamene inu mumamuwona mmodzi akutero. . . Oh, awa ndi oyimba aang'ono aja. Sichoncho izo? Kodi awa ndi amene amayimba? Ine ndimaganiza anali iwo. Chabwino, bwana.

82 Tsopano, dzina lako ndi ndani? [Mtsikanayo akuti, "Ruth."—Mkonzi]. Ruth. Ndi lokongola kwambiri. Ruth ndi dzina lokongola kwambiri. Ndimalikonda ilo, ndimalikonda ilo kwenikweni. Tsopano, ndipo dzina lomaliza lija ndi ndani? Ndi. . . [Winawake akuti, "Myers."] Myers, Ruth Myers wamng'ono, iye ndi mmodzi wa oyimba athu aang'ono kuno. Iwo ndi mapasa? Akuwoneka ofanana kwambiri, sichoncho iwo?

83 Atate athu Akumwamba, ife tikumupereka kwa Inu mtsikana wamng'ono uyu, amene abambo ndi amake akunena kuti sanaperekedwepo mwanjira iliyonse ku utumiki ndi Ufumu wa Mulungu. Ife tikuyika manja pa Ruth wamng'ono, usikuuno, Ruth Myers wamng'ono, ndipo tikupempha kuti Mphamvu ya Mulungu Wamphamvuzonse, Amene wamupatsa iye luso loyimba, ipitirize kumudalitsa iye. Ndipo mulole moyo wake

ukhale woperekedwa kwa Inu, masiku onse amene iye ali pano pa dziko lapansi. Ife tikumupereka iye kwa Inu, mu Dzina la Yesu Khristu.

84 Dzina la mlongo wamng'onoyo ndi ndani? Loyce? Chabwino, Loyce wamng'ono. Mai!

85 Atate Akumwamba, ife tikuyika manja pa Loyce wamng'ono, yemwenso ali ndi luso mu usinkhu waung'ono, kuyimba Uthenga. Mudalitse luso la ana awa, Ambuye. Ndipo tsopano miyoyo yawo ikuperekedwa kwa Inu, ndi makolo awo. Posachedwapa, Ambuye, iwo adzakhala aakulu mokwanira kuti abatizidwe. Pamene iwo adzayambe—pamene iwo adzayambe kuzindikira chimene chiri cholakwika, ndi zinthu, ndi kuyamba kuchita cholakwika, ndiye iwo adzayenera kudzalapa ndi kubatizidwa. Mpaka nthawi imeneyo idzafike, Ambuye, ife tikuwapereka iwo kwa Inu. Mulole mugwiritse ntchito luso lawo kwa ulemelero Wanu. Mugwiritse ntchito moyo wawo, akhale moyo wautali, wachimwemwe, kuti akakutumikireni Inu. Ife tikumupereka mtsikana wamng'ono uyu kwa Inu, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

86 Mulungu akudalitseni inu. Pitani, ndipo Mulungu akhale nanu, ndipo azikudalitsani inu nthawizonse mu chirichonse chimene inu mukuchita.

Izo ziri bwino, M'bale Neville.

Oh, ine—ine ndikungoganiza kuti iwo ndi okongola kwambiri! Ine. . .

87 Atsikana anga ayamba kukula tsopano, chotero ine ndimangoyenera kuti. . .Ine ndinkakonda kuwakweza iwo pansana. Koma iwo akhoza pafupifupi kundiyika ine pansana tsopano, iwo ali chomwecho—aakulu kwambiri; Becky, makamaka, mtsikana wamkulu kwambiri.

88 Tsopano tiyeni titsegule Mawu a Ambuye, ku Mateyu wa 15. . .kapena mutu wa 5. Ndipo tingowerenga gawo chabe, ndipo kenako ine nditenga kuchokera mu izi, Ambuye akalola, mutu waung'ono kwa pafupi fifitini, maminiti twente. Kenako ife tikhala ndi mgonero, ndi kutsukana mapazi, ndi msonkhano wa ubatizo, utitengera ife ku pafupifupi hafu pasiti naini, ndiye, kapena mochedwra pang'ono, kuti titsirizitse. Ine ndikufuna kuti ndiyambire pa mutu wa 5, pa ndime ya 12.

> Sangalalani, *ndipo mukhale okondwera* mochuluka*: pakuti mphotho yanu ndi yayikulu kumwamba: pakuti anazunza chotere*. . .*aneneri amene analipo inu musanakhalepo*.

> Inu *ndi mchere wa dziko lapansi: koma ngati mcherewo* wa*taya kukoma kwake, adzawukoleretsa ndi chiyani?* kuyambira pamenepo *iwo sukhalanso kanthu,*

> *koma kuti utayidwe kunja, ndi . . . kupondedwa pansi* pa *mapazi a anthu.*
>
> Inu *ndi kuwunika kwa dziko lapansi. Mzinda umene* uli *pa phiri sungabisike.*
>
> Ngakhalenso *anthu samayatsa kandulo, ndi kuyivindikira pansi pa mbiya, koma pa choyikapo kandulo; ndipo iyo imapereka kuwala kwa onse amene ali m'nyumbamo.*
>
> Mulole *kuwala kwanu kuwalire pamaso pa anthu, kuti iwo awone ntchito zanu zabwino, ndi kulemekeza Atate anu amene ali kumwamba.*

89 Ine ndikufuna kuti nditenge a—phunziro kuchokera ku ndime yotsiriza imeneyo apo, yomwe ili ndime ya 16: *Mulole Kuwala Kwanu Kuwalire Pamaso Pa Anthu.* "Mulole kuwala kwanu kuwalire pamaso pa anthu, kuti iwo akhoze kuwona ntchito zanu zabwino, ndipo alemekeze Atate anu Akumwamba."

90 Ife tikupeza, mu Lemba, kuti pali malo awiri amene amuna awiri osiyana akuyankhula za kulungamitsidwa. Ndipo mmodzi wa iwo anali Paulo, ndipo winayo anali Petro. Paulo Woyera, ndi Petro Woyera; ndipo Paulo ankamulungamitsa Abrahamu ndi chikhulupiriro, ndipo Petro ankamulungamitsa iye ndi ntchito. Petro ananena kuti iye analungamitsidwa ndi ntchito zake. Paulo ananena kuti iye analungamitsidwa ndi chikhulupiriro chake. Tsopano, iwo sanatsutsane wina ndi mzake. Iwo ankayang'ana pa izo mu mawonedwe awiri osiyana. Ndipo Paulo ankayankhula za chikhulupiriro cha Abrahamu, ndicho chimene Mulungu ankachiwona mwa Abrahamu. Ndipo Petro ankayankhula za ntchito zake zimene zinkayankhula za chikhulupiriro chake. Chotero kwalembedwa, "Ndiwonetseni ine ntchito zanu zopanda chikhulupiriro chanu, ndipo ine ndikuwonetsani inu ntchito zanga za chikhulupiriro changa." Tsopano, chotero, Paulo, powona zomwe ankayankhula, ndi zomwe Mulungu ankaziwona. Ndipo Petro ankayankhula za chimene munthu ankawona, ndipo, chifukwa, ngati munthu akhala ndi chikhulupiriro, iye adzachita monga icho. Moyo wake udzawonetsera izo kwa ena.

91 Chotero ine ndikupita, ndikufuna ndiyankhule pa izo, usikuuno, "Kulola Kuwala kwathu kuwalire."

92 Tsopano, kwa maminiti ochepa awa okha, ine sindikufuna kuti ndingobwera kuno kuti ndingowonedwa kapena kuti ndimvedwe. Izo sizingakhale zabwino. Koma, mwinamwake, Mulungu akandithandiza ine, mwinamwake ife tikhoza kuyankhula mawu ena kwa chinachake chimene chiti chidzakhale chomangiriza kwa ife, chimene chidzatithandize ife tonse, momwe tingachitire bwino ndi kukhala moyo wabwinoko. Ndikutsimikiza kuti izo ndi zomwe ife tonse tadzera pano, ndi

kudzalandira chidzudzulo ndi kudzapeza kumvetsa kwa chimene tingachite kuti tikhale Akhristu abwinoko. Ngati ndiri nacho chinthu chimodzi mmoyo mwanga chimene ine ndimachikhumba, ndi kukhala Mkhristu wabwinoko kuposa yemwe ine ndiri. Ndipo ine ndikutsimikiza uko ndi kulira kwa mtima wa moyo uliwonse umene uli pano usikuuno, ndi kukhala Mkhristu wabwinoko.

93 Nthawi ina kale, ndinkapita kumusi mu msewu, ndipo ine, ndikuyendetsa mothamanga kwambiri, ndipo ndikuyang'ana momwe ndimachitira kawirikawiri, ndekhandekha, ndikuyendetsa. Ndipo kumakhala kuyendetsa kosungulumwa pamene ukuyendetsa wekhawekha. Iwe sungayatse wailesi, pokhapokha ngati pali ena ama netiweki a banja awa kumene ungakapezeko nyimbo zachipembedzo, chifukwa ndi zinthu zonsezo zimene zingachotse Mzimu womwewo mwa iwe.

94 Ndipo kulikonse kumene ine ndimapita, ine nditakalamba pang'ono, bwanji, ine ndimanyamula kapepala kakang'ono. Ndipo pamene Ambuye awulula chinachake kwa ine, ine ndimangochilemba icho. Ndipo ine ndinalemba ngakhale pa mfuti yanga, mu nkhalango, ndi chipolopolo. Ndi zinthu monga choncho, kuti ndingopeza lingaliro limene laperekedwa kwa ine. Kuchotsa kachidutswa ka pa zovala zanga, kapena chinachake, ndi kulemba pa iko. Chinachake chimzake, kuti ndisunge Uthenga mmalingaliro mwanga.

95 Ndipo pamene ine ndinkayendetsa, ndikusesereka msewu uwu, ine ndinawona chikwangwani chachikulu kwambiri chokongola. Ndipo kawirikawiri, inu mukudziwa, iwo amakhala ndi zinthu zambiri zitayikidwa pa zikwangwani izi, koma sindinazindikirepo zinthu zoterozo pa chikwangwani ichi. Kawirikawiri iwo amakhala ndi zithunzi za—za akazi ovala mwatheka, kapena chinachake chimzake, kusasa mtundu wina wa ndudu, kapena—kapena kachasu, kapena mowa, kapena chinachake, zikwangwani zazikulu zowala. Koma chondidabwitsa, kuyang'ana kwanga koyamba, icho chinakopa tcheru changa, chifukwa icho sichinamatidwe ndi chinachake chimzake. Mwayewo sunali pamenepo. Ndipo ine ndinayang'ana mmbuyo, kuti ndiwone.

96 Icho chinali chikwangwani chokongola. Ndipo chitakhala pa malo olondola, basi pamene, pamene iwe ukukhota ngodya iyi, iwe sungalephere kudziletsa kuti usawone chikwangwanicho. Ndipo chodabwitsa changa, icho chinali ndi mawu amodzi atalembedwa pa icho, "Njala?" Basi, "Njala?" Ndizo zonse zomwe zinali pamenepo. Ndiye ine ndinazindikira zilembo zazing'ono pansi pa chikwangwanicho, anati, "Mailosi atatu patsogolo." "Njala? Mailosi atatu patsogolo."

97 Chabwino, ine ndinayamba kuphunzira za izo. Anthu sanali kwambiri . . . Kawirikawiri, ngati ali ndi malo odyera

patsogolo, iwo—iwo amayesetsa kuti agulitse kuposa munthu winayo; chithunzi, nyama zazikulu zopatsa mudyo, ndi zina zotero. Ndipo iwe ukakalowamo, kawirikawiri iwe sumakapeza chirichonse monga amalengezera, koma basi—kusasa basi. Koma ichi chinkawoneka kuti chinali ndi kafikidwe kena.

98 Ndipo ife tikudziwa kuti tsiku lomwe ife tikukhalamo lero, zimapindulitsa kusasa. Ndipo ife tikupeza, kuti, anthu awa amene amachita bwino mmalonda amakhala—amakhala anthu odziwika mu za kusasa malonda. Iwo—iwo amayika izo pa televizioni. Iwo amazipaka izo pa zikwangwani, kulikonse kumene iwo angathe, kuti alengeze malonda awo. "Sutani *iyi*; osati chifuwa mu galimotoyodzadza." Ndi, "Sefa ya munthu woganiza," ndi nsonga ya munthu wina, kapena chinachake chonga zimenezo. Za. . .ndi a. . ."Khalani achangamu, moyo wautali," ndi mowa wawo. Ndi zinthu zonse monga choncho, ndi kusasa malonda. Ndipo iwo amachotsa msonkho wochuluka wa ndalama zomwe amapeza, basi ndi cholinga chakuti asase malonda. Ndipo izo ndithudi zimawapindulira.

99 Chotero ngati izo zimapindulitsa, kuchita izo, ine ndinayamba kuganizira, "Ndiye Chikhristu sichingapindulitse bwanji ngati icho chitasasidwa malonda?"

100 Chabwino, ine ndinaganiza, ndiye, "Chiyani—kusasa malonda ndi chiyani?" Inu mukuyenera kukhala ndi chinachake chimene chiri chosiyana pang'ono ndi chomwe ena onse ali nacho, kapena ngati icho chiri chawamba, monga zinthu za mdziko, icho sichidzakopa konse tcheru cha anthu. Tsopano, ngati munthu angakhale kuti akufunafuna galimoto, iye angachipitirire chikwangwani chimenecho. Koma ngati iye atakhala kuti ali ndi njala, iye angakhale akufunafuna chikwangwani chimenecho.

101 Chotero ine ndikukhulupirira kuti Mkhristu ndi chikwangwani cha Mulungu. Ine ndikukhulupirira kuti aliyense wa ife ndi chikwangwani cha Mulungu. Ndipo ife sitikuyenera kumachita zochuluka za kumangotengeka za izo, monga ife timachitira. Basi mophweka tizingokhala moyo umene ungawapangitse anthu kukhala ndi njala kuti akhale monga inu.

102 Tsopano, ine ndinazindikira pa chikwangwani ichi, chinachake ichi, icho sichinanene chirichonse, palibe, koma kungofunsa funso, ngati muli ndi "Njala?" Ndipo simungamugulitse aliyense chirichonse choti adye pokhapokha ngati ali ndi njala. Chinthu choyamba chimene kusasa malonda kumachita, munthu amene akudutsapo akuyenera kuchiwona icho.

103 Tsopano, njira yokhayo imene dziko liti lidzamuwonere Khristu ndi pamene iye, iwo, amuwona Iye mwa inu ndi ine. Ndiyo njira yokhayo imene iwo ati adzamuwonere konse

Khristu. Chawo—chikumbumtima chawo chimachita dzanzi mpaka kulowa kwa dzuwa, ku kuyitana kwa mbalame, mpaka ku masamba, ndi—ndi udzu, ndi maluwa; ndi nyimbo, ndi Uthenga ndi zina zotero, zimene ife timasangalala nazo ife tikamupeza Khristu. Koma, mpaka ife titafika pa malo amene ife tikumuwonetsera Khristu!

104 Tsopano, mukumbukire zimenezo. Aliyense wa inu, kuyambira usikuuno, mukumbukire, ndinu zikwangwani za Mulungu. Ndipo ndinu—ndinu ndi osasa malonda wa Mulungu. Tsopano, dziko lidziyang'ana pa inu, kuti liwone chimene Khristu ali. Chotero ife sitikufuna kuyika zinthu zambiri pamenepo, zomwe zimachitira umboni za zinthu zomwe ife sitiri. Tiyeni tikhale chimenecho poyamba. Ndiye pamene ife tikhale chimenecho, ndiye dziko lidzamuwona Khristu mwa inu ndi ine.

105 Chinthu choyamba, chimene, kusasa kulikonse, munthu akuyenera kuchiwona icho.

106 Kenako, chinthu chotsatira, iwo akuyenera kuchifuna icho. Tsopano, ngati iwo achiwona icho ndipo osachifuna icho, ndiye izo nzosiyana. Koma inu simunayike kusasa malonda kopanda pake.

107 Koma ngati iwo, choyamba, akuyenera kuti achiwone icho, ndipo kenako ife tikuyenera kuchipanga icho kukhala chokopa kwambiri kwa iwo. Oh, ine ndikuyembekeza ife tikuziwona izo, kukopa kwa chipulumutso, chimene icho chimachita kwa munthuyo. Ife tikuyenera kulikopera dziko kwa Khristu. Ndipo Uthenga umakhala ndi kukopa. Iwo uli nako iko kwa iwo amene ali ndi njala ya Mulungu. Iwo umangowakopa iwo amene ali ndi njala ndi ludzu, ndipo amenewo ndi amene ife tikuwafuna. "Palibe munthu angakhoze kubwera kwa Ine, kupatula Atate Anga atamukoka iye."

108 Koma alipo ochuluka kwambiri amene Atate awakoka, ndipo ali ndi njala ndi ludzu kuti amupeze Mulungu, ndipo komabe sakudziwa komwe angakamupeze Iye, chifukwa iwo amene akuyenera kukhala zikwangwani amatidwa kwambiri ndi zinthu za mdziko, mpaka iwo sangakhoze kuwona kumene iwo anali nazo zochuluka kuposa zomwe iwo anali nazo iwo asanabwere kwa Iye. Iwo amakhala ngati dziko. Amayankhula ngati dziko. Amayimba nyimbo zomwezo zimene dziko limayimba. Iwo amavala ngati dziko, ndikutanthauza, makamaka mwa akazi. Ndipo iwo amachita ngati dziko. Iwo amapita ku malo achidziko. Amapita ku zisangalalo za chidziko.

109 Winawake ananena kwa ine, tsiku lina, za mtumiki wina. Ndipo ine ndimamukonda mwamunayo. Palibe kukaikira koma chimene iye ndi munthu wopambana. Iye anati, "Koma iye ananena kuti—kuti inu munali woyera wodzigudubuza," kwa ine, kuti ine ndinali woyera wodzigudubuza.

110 Ine ndinati, "Chabwino, ine—ine—ine sindikuganiza kuti ine ndiri. Koma," ine ndinati, "Ine—ine ndikufuna kukhala woyera. Ndipo ngati Ambuye akanandiuza ine kuti ndigubuduke, ine ndikuganiza ndikanagubuduka. Koma ine—ine ndikufuna kuti ndikhale woyera, mulimonse, ndikhale moyo *wachiyero*, zikutanthauza 'kuyera pamaso pa Mulungu.'"

111 "Ndipo chotero iye anati, chabwino, kuti inu mumapita kunja, kutsidya kwa nyanja, ndi kumazungulira monga choncho, ndipo mwadzipanga nokha wamishonare. Palibe mpingo umene unakutumizani inu, ndipo inu munangodzipanga nokha wamishonare wopangidwa ndi manja."

112 "Chabwino," ine ndinati, "ngati ndikanazipanga mishonare wopangidwa ndi manja, izo sibwenzi zikukopa tcheru cha dziko, chifukwa iwo sakufuna izo. Iwo akufuna Khristu."

113 Ndipo ife tikupeza, kuti, amuna amenewo ndi anthu amene amaganiza zinthu zimenezo. . .Pali magulu awiri osiyana; Mulungu ali ndi magulu awiri osiyana.

114 Pali amuna amene Mulungu amawagwiritsa ntchito kukhala kunyumba, ndi kumasangalatsa odwala, ndi kuyika akufa, ndi kupsyopsyona ana, ndi kukwatitsa achinyamata awo, ndi zina zotero monga choncho. Ambiri a amuna amenewo sadziwa kuti kunyamula lupanga ndi chiyani, ndi kupita kunja uko ndi lupanga logwira manja awiri kutsogolo. Iwo samadziwa chimene nkhondo ili, kumenyana ndi mdani. Iwo amatuluka kunja kuno, ndipo iwo ndi amuna anzeru, afioloje, amuna opambana, amene akhoza kuyima, kuyika ulaliki umene uli wokhudza kwambiri, ndipo akhoza kuyankhula ndi chinenero choterocho, mpaka Webster osadziwa konse zomwe iwo akunena. Iwo ali ndi madigiri ku koleji, koma zimenezo ndi zabwino pamene iwe ukuyankhula kwa gulu laluntha lomwe likungofuna mpingo wakwawo.

115 Koma pamene inu mufika kunja uko ku bwalo la nkhondo, kumene amuna amenewo amakhala ndi zochuluka kuposa zimenezo, iwo amayenera kuti aziwona Mphamvu ya Mulungu Wamphamvuzonse ikuwonetseredwa, kapena inu simudzagulitsa konse iyo kwa iwo. Iwo akuyenera kumuwona Khristu mu chiwukitsiro Chake. Inde, bwana.

116 Amuna amenewo samadziwa chomwe chiri kugwira Lupanga logwira ndi manja awiri, nkumamenyana chala ndi chala ndi mdani kumeneko. Kumene adierekezi ndi asing'anga, ndi china chirichonse, atayima pamenepo, amakutsutsa iwe pa dzanja lirilonse. Ndi kumene anthu, amene amawerenga Baibulo limenero, amati, "Ngati Yesu Khristu ali yemweyo dzulo, ndi kwanthawizonse, ndiloleni ine ndiwone Mzimu Woyera ukuchita monga Iwo unkachitira kumbuyo uko." Mwaona? Ndiye iwe sungatenge a—maphunziro ndi kuchita zimenezo.

117 Zimatengera Mphamvu ndi chiwukitsiro cha Yesu Khristu kuti zibale izo. Inde. Ndipo tsopano ndi zomwe mbadwa zanjala zimayang'ana. Iwo akuyenera kuwuwona Iwo, ndipo iwo akuyenera kuwufuna Iwo.

118 Ndipo ndicho chinthu chomwecho chimene fuko lino liri nacho. Ndi chifukwa chake, usikuuno, chimene ife tiri ndi machenjezo onse awa a nkhondo ya atomiki, ndi chifukwa chakuti mafuko awuwona Iwo, fuko lino latero, ndipo sakuwufuna Iwo. Ndi chifukwa chimene chiweruzo cha Umulungu chiri pa iwo. Ndi chifukwa chakuti ife tiri mkati, tayezedwa pa muyeso.

119 Ine ndinawona pamene Purezidenti wathu, Bambo Kennedy, Tom, ine ndikukhulupirira dzina lake ndi, Kennedy, amene anatumiza ku izi, asirikali ochuluka kwambiri, ku nkhondo iyi ya tsankho. Iye anatumiza foro handirede ndi chakuti, uko Kummwera, kuti akayimitse nkhondo ya tsankho iyi. Ndipo pamene iye anatsiriza, pa ulendo wake wathunthu, iwo sakanakhoza kutumiza kenanso, iye anali nawo ndendende sikisi handirede ndi sikisite-sikisi. Izo zinali mu magazini ya *Time's*. Oh, ngati anthu akanangokhala auzimu, akanadzuka ndi kuwona chimene "sikisi handirede ndi sikisite-sikisi ili." Ndendende zomwe iwo anali nazo. Izo ziri mu *Time's* ya mwezi uno.

120 Tsopano, ife tikupeza, kuti, mpaka anthu anayamba kumufuna Mulungu, mpaka anthu anayamba kuchita ludzu! Yesu anati, "Odala ndi iwo akumva njala ndi ludzu la chirungamo, chifukwa iwo adzakhuta." Tsopano, iwe ukuyenera kuchita njala ndi ludzu lofuna Iwo.

Ndife zikwangwani za Khristu.

121 Ndipo Khristu ndi wotithandizira wathu, pakuti thandizo ili ndi la mwa Khristu. Ndipo Iye akutipatsa ife Moyo wathu, kuti timuthandizire Iye. Tsopano, kodi inu mungakhale munthu wamtundu wanji ngati muthandizira winawake? Kodi ife tikuyenera kukhala munthu wa mtundu wanji—tikuthandizidwa ndi Khristu? Iye amatipatsa ife chipulumutso. Iye amatipatsa machiritso athu. Iye amatipatsa thanzi ndi mphamvu. Ndipo Iye amatipatsa chakudya chathu. Iye amatipatsa nyumba zathu. Ndiye, ife timathandizidwa ndi Khristu. Ndipo anthu achipentekoste, amene ali odzazidwa ndi Mzimu Woyera, ndi othandizira a Yesu Khristu. Iwo athandizidwa ndi Yesu Khristu, ndipo apatsidwa Mzimu Woyera, kuti akhale chitsanzo kwa anthu.

122 Kodi ife tikuyenera kukhala chiyani, lero? Kodi Mpingo ukuyenera kukhala kuti, lero? Tikuyenera kukhala chomwecho, mu chikhalidwe chimenecho, chimene chingapangitse dziko lonse kukhala lofuna kukhala monga ife. Chifukwa anthu amapita mumsewu ndipo amati, "Apo pali munthu, ine ndikhoza

kusagwirizana ndi iye, pa Chiphunzitso chake chachipembedzo. Koma ine ndikukuuzani inu chinthu chimodzi, ameneyo ndi Mkhristu weniweni." Akuyenera kukhala akazi akupita mu msewu, akuti, "Iye akhoza kumawoneka wachikale. Iye akhoza kusakhala monga akazi ena onse awa amene mukuwawonawa. Koma pali Mkhristu m'modzi mtawuni muno, ngati alipo mmodzi, ndi uyo akupita apoyo." Chifukwa, ife timathandizidwa ndi Yesu Khristu. Ameni.

123 Oh, kodi angakhale munthu wa mtundu wanji amene, ife tikuyenera kukhala, ngati ife tiri zikwangwani Zake ndipo ndife othandizidwa ndi Iye? Ndiye, mwa Khristu, ndi Mmodzi kumene ife timapezako Moyo wathu, ndipo ife timapeza mphamvu zathu, ndipo ife timapezako zonse zimene tiri nazo, zimachokera kwa Khristu. Iye ndi wotithandizira wathu. Oh, ndine wothokoza kwambiri chifukwa cha izo!

124 Chotero, ife tikuyenera kukhala monga Iye. Tizikhala osamalitsa zimene ife tikuchita, zimene ife tikuyankhula, zimene ife tikuchita m'moyo wathu wa tsiku ndi tsiku, chifukwa ife tikuthandizidwa ndi Khristu. Kodi ife tikuyenera kuti tiziyenda chotani ngati tikuthandizidwa ndi Khristu? Kodi ife tikuyenera kumanena chiyani ngati tikuthandizidwa ndi Khristu? Ngati winawake anena choipa kwa ife, kodi tikuyenera tizinena chiyani ngati timathandizidwa ndi Khristu? Ife tikuyenera tizikhala monga Khristu. Kodi sikulondola kumeneko?

125 Tsopano, tsopano, pali chinthu chimodzi chokha. . . Ndipo chinthu china chimene ife tikuyenera kuchita, osati chinthu chokhacho, koma chinthu china chimene ife atumiki tikuyenera kuchita. Ife tikuyenera tizilalikira Uthenga umene uli wokopa kwa anjala.

126 Tsopano, ngati timalalikira Uthenga wa chisangalalo, ndi kumanena kuti, "Chabwino, inu mukuyenera kubwera mudzajowine chipembedzo chathu. Ife tinali ndi foro sauzande owonjezera chaka chathachi, mu bungwe lathu." Izo si zimenezo. "Chabwino, ngati inu mungabwere ku tchalitchi changa, kapena kudzakhala membala wa tchalitchi changachi, ife tidzawonetsetsa kuti mukusamalidwa mu. . . mukadzakalamba. Ndipo inu mukhale membala wokhulupirika, ziri ngati inshulansi, mudzasamalidwa mukadzakalamba. Ife tidzawonetsetsa zimenezo." Izobe si zokoperazo.

127 Chinthu chimene ife tikuyenera kuchita ndi kulalikira Uthenga umene uli wokopa kwa dziko lanjala.

128 Tsopano, mungakope bwanji dziko lanjala limene likufuna kuwona komwe iwo anachokerako, chimene iwo ali, ndi kumene iwo akupita, pokhapokha inu mutalalikira Uthenga umene umamudzutsa Khristu mmwamba mu chikhalidwe chamoyo, pomwe pano motizungulira ife tsopano? Ife sitingakhoze kuchita zimenezo. Palibe njira ayi. Ife, ife tikhoza kujowina, ife tikhoza

kujowina a Masons, a—Odd Fellows, kapena loji iliyonse, kujowina loji ina zikhoza kukhala zabwino.

129 Koma ife tikuyenera kulalikira Uthenga umene uli wokopa kwa anthu anjala, umene udzagwire iwo amene ali ndi njala ndi ludzu la chirungamo. "Odala ali iwo akumva njala ndi ludzu la chirungamo, chifukwa iwo adzakhutitsidwa." Tsopano, kodi iwo angakhale chotani? "Olungama azadzazidwa." Kudzazidwa ndi chiyani? Mzimu Woyera.

130 Baibulo linati, "Stefano anali munthu wodzaza. . . " Wodzaza ndi chiyani? Wodzaza ndi mphamvu. Wodzaza ndi chikhulupiriro. Wodzaza ndi chikondi. "Wodzaza ndi Mzimu Woyera." Icho ndi chimene chinamupanga iye chimene iye anali, ndi chifukwa iye anadzazidwa ndi Mzimu Woyera. Iye anali chikwangwani chenicheni chosasira malonda a Khristu.

131 Pamene iye anayima pamenepo, mmawa uja, pa mabwalo a milandu a Sanhedrin, ndipo iwo nkumamutsutsa iye. Iwo anati, "Munthu uyu," zonse zomwe iye amachita. Ndipo iye anayima yekha, iye yekha basi, uko pamaso pa bwalo lamilandu lalikulu la Sanhedrin. Mwinamwake Ayuda thuu kapena firii sauzande, kapena faivi sauzande, atayima pamenepo ndi chala choloza.

132 Baibulo linati, pamene iye anapita kunja uko, kuti, "Nkhope yake inkawoneka ngati Mngelo." Izo sizikutanthauza kuti iye anali ndi Kuwala kukuwala pa nkhope yake. Mngelo akanakhala mtumiki amene ankadziwa chimene iye ankachikamba. Stefano anapita kumeneko, osawopa imfa. Iye sankawopa kalikonse, chifukwa iye ankadziwa chimene iye ankanena.

133 Monga Paulo anati, "Ine ndikumudziwa Amene ndamukhulupirira, ndipo ndine wokakamizika kuti Iye ndi wokhoza kusunga icho chimene ine ndachipereka kwa Iye."

134 Koma Stefano anapita kumeneko, pamaso pa bwalo lamilandu la Sanhedrin, monga nkhosa pakati pa gulu la mimbulu, ikulirira magazi ake. Ndipo iwo anamutsutsa iye, ndi kumaloza chala chomuyimba mlandu. Kodi iye anachita chiyani? Iye anati, "Amuna ndi abale, Mulungu wa ulemelero anawonekera kwa atate athu, Abrahamu, pamene iye anali akadali mu Mesopotamia, iye asanayitanidwe kuti atuluke." Anapitirira ndipo anaibweretsa iyo pansi, mbiriyakale yonse ya Abrahamu, ndi momwe kuti kudzera mwa iye akanadzabweretsa Amitundu. Ndipo pamene iye anafika ku malo enaake. . . Tamuwonani iye, wodzazidwa ndi Mzimu Woyera. Iwo akanakhoza, kudikirira, sanathe kudikirira mpaka iwo anayika manja awo pa iye. Iye anati, "Inu a makosi owuma, osadulidwa mu mtima ndi makutu, inu nthawizonse mumawukaniza Mzimu Woyera. Monga makolo anu anachitira, inunso mukutero." Iye anali chikwangwani chosasa malonda a Mulungu.

135 Ndipo pamene iwo anamugenda iye mpaka kumupha, anamuponyera iye kunja kwa mzinda ndipo anakamumenya iye

mpaka kumupha ndi miyala, pamene iye ankafa, anakwezera mutu wake Kumwamba ndipo anapempha chikhululukiro kwa iwo amene ankamugenda miyala, chimodzimodzi monga momwe Yesu anachitira pa mtanda.

136 Kenako, Mulungu anawona chikwangwani Chake chaching'ono chosasira malonda chikuchotsedwapo. Stefano anayang'ana Kumwamba, anati, "Taonani, ndikuwona miyamba itatseguka, ndipo Yesu akuyima kudzanja lamanja la Mulungu." Ndipo iye anagona tulo m'mikono ya Mulungu. Anali chikwangwani chosasira malonda kwa dziko lanjala.

137 Inu mukuti, "Chabwino, ndi angati anali kumeneko? Inu munati kunali mwinamwake faivi sauzande. Ndi angati a iwo anapulumutsidwa?"

138 Kunali mmodzi. Iye sanavomereze izo nthawi imeneyo, koma zaka mtsogolo. Aleluya! Penapake, chikoka chanu sichimafa. Panali mmodzi yemwe ananyamula chikhotho, Saulo, Mfarisi wamng'ono uja atayima pamenepo, anafunsira ndipo anachitira umboni ku imfa yake. Koma pamene anawona kulengeza kuja kwa Mphamvu ya Khristu wowukitsidwa mwa munthu wamng'ono ameneyo, izo sizinachoke kwa iye. Munthu yemweyo, Paulo, mmodzi uja atayima pamenepo mmawa umenewo, anatsogolera ma teni amasauzande a miyoyo kwa Khristu, chifukwa munthu mmodzi anali wololera kupereka moyo wake kukhala chikwangwani chosasira malonda a Yesu Khristu.

139 Kodi ife tikuyenera kuchita chiyani lero? Ziribe kanthu, sitikusowa kukhala ndi omvetsera ambiri. Ife sitikusowa kulalikira kwa teni sauzande. Sitikusowa ngakhale kulalikira. Ife tikhoza kukhala chikwangwani chosasira malonda a Mulungu. Mukudziwa bwanji kuti moyo wanu sungathe kumuyambitsa mnyamata wina pa Uthenga? Ena a inu amuna achikulire, onani akazi okalamba, akumuyambitsa mnyamata wina pamunda kunja uko, mungapindulire miyoyo teni sauzande kwa Khristu, chifukwa kuti iye anawona Khristu mwa inu, kuti inu munamupereka Khristu kwa iye, mu Mphamvu yophweka ya Uthenga. Inde.

140 Ndikuganiza kuti tikumufuna Khristu. Inde, bwana. Njira yokhayo imene ife timamuwonera Khristu ndi pamene Iye adzinyezimiritsa mwa wina ndi mzake. Ine ndimamuwona Khristu mwa inu. Inu mumamuwona Iye mwa ine. Umo ndi momwe timamuwonera Khristu. Ine ndimabwera ku msonkhano. Ndikayamba kulalikira. Ine ndimawayang'ana anthu. Iwe ukhoza kuwona ngati iwo ali ndi chidwi kapena ayi, maminiti ochepa chabe. Iwe umayang'ana pa omvetsera anu. Iwe utha kudziwa ngati ukuwatopetsa iwo kapena ayi. Mukuona? Ndipo chinthu choyambirira inu mukudziwa, iwe umawawona iwo atakhala pamenepo, akukangamira ku Mawu

aliwonse, pansi pa kuyembekezera. Mukuona? Ine ndikuwona Khristu akunyezimiritsidwa mwa munthu ameneyo, chifukwa iye akuchitira njala ndi ludzu la kwa Mulungu.

141 Ndiye, ine, ndikamalalikira Uthenga, iye amamuona Khristu akunyezimiritsidwa mwa ine. Ine ndimamuwona Khristu akunyezimira mwa iye. Izo zikutanthauza kuti Khristu ali pakati pathu ndiye. Ameni. "Kuchita njala ndi ludzu." Ine ndimawawona omvetsera, momwe iwo akuzitengera izo. Ndimanena chinachake chimzake, ndimapenya chimene—zotsatira zimene Iwo ukutengera pa iwo. Ndimawona nkhope zawo zikuwala, zodzaza ndi chisangalalo. Iwo amakhala takonzeka pamenepo kuti alandire chinachake. Ameneyo ndi Khristu. Ine ndimawona Khristu akunyezimira mwa munthu ameneyo chifukwa Uthenga, Uthenga wophweka wa Khristu, ukugwira mu mtima umenewo, chifukwa iwo ali ndi njala ndi ludzu.

142 Ndipo ine ndawonetsa chikwangwani apa, kusasa malonda. Kusasa malonda kwamtundu wanji? Osati fioloje ina, osati kachikhulupiririro kena kopangidwa ndi munthu, koma kwa Khristu amene akukhala moyo basi chimodzimodzi lero, monga Iye anali kumbuyo uko, pakuti Iye ali yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ameni. Kulondola. Iwo amaiwona mphamvu imeneyo ya Mulungu ikusuntha, kukuwona Iko mchipinda, ndi kukuwona Iko kukuwaitana anthu, kuzindikira mitima yawo, kuchiza odwala, kuwulula zinsinsi za mtima wawo, kutsegula makutu ogontha, kuwapangitsa akhungu kupenya. Ndi chiyani icho? Iko ndi kukopa. Ndi chikwangwani cha Khristu. Ndipo anthu amakuwona Iko, ndipo iwo amasonkhana, ndipo amamutamanda Mulungu. Ine ndimakuwona Iko mwa iwo pamene iwo akumutamanda Mulungu. Iwo amakuwona Iko apa, pamene Iko kukupita njira iyi. Chotero, kudzera mwa wina ndi mzake, ife timawona Khristu akunyezimiritsa Kuwala Kwake. Tsopano, ziribe kanthu kuchuluka kwa momwe ine ndingakhoze kunyezimiritsa Iko *apa*, pokhapokha Iko kutanyezimiritsa pa inu, nanunso, ife sitidzakumvetsa konse Iko.

143 Uthenga udzakhala wopanda mphamvu pokhapokha winawake atakhala pamenepo kuti awutenge Iwo. Adzakhalapo ochuluka amene sadzawutenga Iwo. Koma iwo amene ati adzawutenge Iwo, Iwo udzanyezimiritsa mwa iwo.

144 Analipo mwinamwake faivi sauzande mmawa umenewo pa kuphedwa kwa Stefano, koma analipo mmodzi amene Iwo unanyezimiramo. Ngakhale kumapeto kwa moyo wake, iye ananena pamenepo, "Ine siwoyenera nkomwe kutchedwa mmodzi wa oyera," iye anati, "chifukwa ndinazunza Mpingo wa Mulungu, ngakhale kufikira imfa." Kuvomereza kwake ku kugendedwa kwa wofera ameneyo, Stefano, sikunachoke konse kwa Paulo. Iye anati, "Ine ndinauzunza Mpingo, ngakhale

mpaka imfa." Mukuona? Izo sizinachoke konse kwa iye, chifukwa iye anamuwona Khristu akunyezimiritsidwa.

145 Kodi Stefano anachita motani izo? Iye sanachite zozizwitsa zirizonse, ngakhale iye ankadziwa kuti Khristu anali wochita zozizwitsa. Iye ankadziwa mphamvu zonsezi ndi zinthu. Koma kodi iye anachita chiyani? Iye anangowupereka moyo wake mwanjira yakuti iwo anawona kuti inali mphamvu ya Khristu. Ameni.

146 Inu mukhoza kusawona masomphenya. Inu mukhoza kusaika manja anu pa munthu wodwala, ndi kumverera mphamvu ya Mulungu Wamphamvuzonse ikupanga chigaza cha munthu kukhalanso ndi moyo. Inu mukhoza kusamuwona Iye atayima kutsidya mu mautaaleza atatu kapena anayi. Inu mukhoza kusawona chifaniziro Chake. Inu mukhoza kusamvera konse liwu Lake. Komabe inu mukhoza kukhala chikwangwani chimene chidzanyezimiritsa Yesu Khristu, ndi moyo umene wakhala wangwiro ndi wosayipitsidwa ndi dziko. Osaunjikika ndi zinthu zodetsedwa mozungulira moyo wanu; koma chinthu choyera, kuti icho chidzapangitsa mtima wanjala kukhala ndi njala ndi ludzu kukhala monga inu. Ameni.

147 Inu ndi mchere wa dziko lapansi. "Ngati mcherewo utaya kukoma kwake, adzaukoleretsa ndi chiyani?" Uko nkulondola. Kuchitira njala ndi ludzu! "Mulole kuwala kwanu kuwalire pamaso pa anthu, kuti iwo akhoze kuwona ntchito zanu zabwino, awone zimene inu mukuchita, ndi kulemekeza Atate amene ali Kumwamba." Kuchitira njala! Zikwangwani! Kunyezimiritsa! Zodabwitsa! Inde, bwana.

148 Tsopano, nafenso, ife sitikufuna kuchita izi. Ife sitikufuna kugulitsa izo mwaliwiro, kungoti, "Chabwino, ine ndinatembenuka usiku watha. Aleluya! Dziko lonse lapansi. . . " Inu simungachite zimenezo. Kumeneko ndi kugulitsa mwaliwiro. Ngati ife tingachite zimenezo, chinthucho sichabwino kwambiri. Ngati munangokhala abwino, ndikuti, "Ine ndikudziwa nthawi ina, ine—ine ndinakhala wabwino kwa masabata awiri nditatembenuka mtima. Ine ndinakhala awiri, ndinakhala—ndinakhala masabata awiri, moyo wangwiro basi." Ndiko kugulitsa mwaliwiro. Izo ziri ngati Hadacol uyu amene tinali naye, palibe kanthu koma mulu wa mavitamini atakulungidwa pamodzi, ndipo izo sizinakhalitse koma kanthawi kochepa. Iye potsiriza anatha.

149 Mukufuna kukhala Mkhristu wa tsiku ndi tsiku, Mkhristu wa ora lirilonse, Mkhristu wa chaka chirichonse, osati wogulitsa mwaliwiro. Koma mulole Kuwala kwanu kuwalire.

150 Ngati inu mungapite kwa munthu ndikumupempha iye kuti alandire Khristu, iye nkukusekani pamaso panu, musachokepo ndikuti, "Chabwino, palibe kanthu kwa Iwo, kapena iye

akanawavomereza Iwo." Ayi. Ndiko kugulitsa kwa Hadacol. Ife sitikugulitsa Hadacol.

151 Ife tikugulitsa Uthenga, mphamvu ya Mulungu wamoyo, Khristu yemweyo dzulo, lero, ndi kwanthawizonse. Ngati dziko lapansi likudani inu, iwo anamuda Khristu asanakudeni inu, pa chifukwa chomwecho iwo anamupititsa Iye pamtanda. Koma ndife omuyimira Ake. Ndife zikwangwani Zake. Ife timamusasa Iye malonda.

152 Sitikusowa kukhala ndi zinthu zambiri zapamwamba, zambiri za, "Dokotala, Ph.D., LLD.! Mpingo waukulu, woyeretsedwa wa *Wakuti-ndi-wakuti* ndi *Wakuti-ndi-wakuti*, unakhazikitsidwa kale mmbuyo mu *chakuti-ndi-chakuti* ndi *chakuti-ndi-chakuti*! Ife tiri ndi *chakuti-ndi-chakuti* ndi *chakuti-ndi-chakuti*!"

153 Zimangowapangitsa iwo kumva njala. Ameni. Chikwangwani chophweka, choyera ndi Khristu atalembedwa mmoyo wanu wonse, "Kuti anthu adzawone ntchito zanu zabwino ndipo adzalemekeze Atate amene ali Akumwamba." Ndi zimenezotu.

154 Musadzazidwe ndi zinyalala za mdziko. Musayesere kudzisasa nokha malonda monga momwe wina amanenera, "Chabwino, ine ndine wa *Akuti-ndi-akuti*, mpingo waukulu uwu. Iwo ndi mpingo waukulu kwambiri mu mzinda."

155 Ife tiri ndi munthu pafupi ndi dera lathu uko, amene anasiya mpingo waung'ono kumtunda kuno pa msewu waukulu, kuti apite ku tchalitchi chachikulu, chifukwa, iwo anati, "Gulu labwino la anthu limapita kumeneko." Gulu labwino la anthu? Mukuona? Sakudziwa ayi. Wawo—ubongo wawo umatuwa. Ndi—iwo—wasokonezedwa ndi zinthu za mdziko. Gulu labwinoko la anthu?

156 Kodi gulu labwino la anthu ndi chiyani? Anthu amene abadwa mwa Mzimu wa Mulungu. Ngati iwo ali osauka kwambiri sakudziwa komwe chakudya chotsatira chiti chichokereko. Limenero ndiro gulu lokhalo la anthu limene liri loyenera chirichonse. Amenewo ndi anthu amene abadwa kachiwiri.

157 Pamene Yesu anabwera, ndi gulu la mtundu wanji la anthu limene Iye ankayenera kulitenga? Osaphunzira, asodzi, amuna . . . Petro, mtumwi, woyera wamkulu amene anapatsidwa mafungulo Akumwamba, samakhoza ngakhale kusayina dzina lake lomwe; akununkha ndi nsomba zochokera ku utsi wakale wa nsomba ndi zinthu, atavala apuloni yakale yanoninoni. Yesu anatenga mtundu umenewo wa munthu. Lero, iwo angamuthamangitse iye mu mpingo ngati iye angabweremo, kulondola, kuti adzapembedze. Mukuona?

158 Anthu akufunafuna "upamwamba." Ndipo kodi mukudziwa kuti satana amakhala mwapamwamba? Kodi mukudziwa

chimene chinayambitsa nkhondo yoyamba Kumwamba? Panali pamene Lusifara anakhazikitsa gulu lapamwamba la anthu, anapeza gulu lapamwamba la Angelo, iye ankaganiza. Waukulu, ufumu wokulirapo, ufumu wowala kwambiri, wonyezimira kuposa umene Mikaeli anali nawo. Ndipo iye anathamangitsidwa Kumwamba. Mukuwona kumene upamwamba umachokerako? Muzikhala kutali ndi upamwamba.

159 Anjala samafuna upamwamba. Wanjala amafuna chakudya. Inde, bwana. Ozizidwa amafuna moto, osati chithunzi, cha moto. Ndipo wanjala, akumva ludzu la Mulungu, amafuna Uthenga ndi mphamvu ya Yesu Khristu. Ameni. Ziribe kanthu momwe izo ziliri zophweka, momwe—momwe kusa-. . .momwe ziliri zosatchuka ndi dziko, iwo amafuna zenizeni.

160 Munthu amene akufa, munthu amene akudziwa kuti akuyenera kukakumana ndi Mulungu, samasamala za upamwamba uliwonse. Iye amafuna kumupeza Mulungu. Iye amafuna kupeza chitsimikiziro, kuti pamene adzafika pa mtsinje, padzakhala winawake kumeneko woti adzakumane naye iye ndi kudzamuwonetsa iye njira. Iye amafuna chinachake chimene chimamuzika iye tsopano, amene amadziwa, "Ine ndikudziwa Muwomboli wanga ali moyo. Pa masiku otsiriza, Iye adzayima pa dziko lapansi."

161 "Ndine wokakamizika kuti palibe chomwe chiripo, chimene chiri chamtsogolo, kapena chimene chikubwera, njala, zowopsya, kapena china chirichonse, chingakhoze kutilekanitsa ife ku chikondi cha Mulungu chimene chiri mwa Khristu." Izo ndi zimene iwo amafuna, amafuna chinachake chimene. . .

162 Osati kudzipangitsa kukhulupirira, chinachake chogulitsa mwaliwiro, "Ndipo bwerani kuno ndipo mudzajowine mpingo uwu." Ine ndikufuna chinachake chimene. . .Kunena, "Chabwino, ine ndipita uko ndi kukajowina mpingowo. Ndidzakhala ndi msonkhano wodzipereka, abusa adzandibatiza mwachinsinsi ndi kudzanditengera mu tchalitchi." Ayi, ayi. Izo si zimenezo ayi. Ichi ndi chimodzi mwa zinthu zogulitsa mwaliwiro. Sizitenga nthawi yayitali.

163 Ine ndikufuna kutembenuka kwa kachitidwe kachikale kenikeni, mwamuna kapena mkazi amene ali wololera kutuluka ndi kunena, "Ine ndalakwitsa. Ine ndikufuna kukhala monga woyandikana naye wanga. Ndimalakalaka nditakhala mkazi ngati woyandikana naye wanga. Ndikufuna kukhala mwamuna ngati woyandikana naye wanga. Ine ndikufuna kuti ndiziyenda mwaumulungu kwambiri pamaso pa anthu, kuti anthu aziganiza za ine mofanana ndi momwe iwo ankachitira za iye. Ndikufuna kukhala monga Yesu Khristu."

164 Tsopano, kumbukirani, potseka, ine—ine—ine ndimangopitirira. Koma, potseka, ine ndikufuna ndinene

ichi: Ife si ogulitsa malonda Ake, ndife zikwangwani Zake. Mukuona? Musaganize kuti ndife ogulitsa Ake. Iye samasowa wogulitsa malonda aliyense, zikwangwani basi.

165 Ine ndinkagwira ntchito ku Public Service Company. Ndipo tinali ndi nyali ya Mogul iyi. Iwo anali ndi mpikisano pa iyo. Aliyense amene anagulitsa nyali zambiri, ankalandira, oh, mphotho, ndi zina zotero, ndi peresenti inayake, iwo amalandira akagulitsa. Chabwino, munthu aliyense, wogwira ntchito aliyense, ankayenera kukhala wogulitsa nyali izi. Chabwino, ndinayamba kuganiza za chinachake chonga ichi, "Ngati katunduyu ali wodalirika kwa ine, kampani ikuidalira nyaliyo. Tsopano, ngati nyali imeneyo ili yabwino mulimonse, iyo idzigulitsa yokha. Ndipo ngati iyo siyabwino, ndiye ndikuyika chinachake pagulu chomwe sichiri chabwino."

166 Ine sindinkakhulupirira konse mu zimenezo. Ine sindimakhulupirira mu zinthu za amalonda opanikiza kwambiri. Ndi chifukwa chake ine sindimakhulupirira izo mu chipembedzo. Ngati ine ndiri ndi chinthu chimene chiri chabwino, icho chidzigulitsa chokha. Uko nkulondola. Icho chidzigulitsa chokha.

167 Ndiye inu mukudziwa chimene ine ndinachita? Ine ndinapita kumeneko, ndipo ine ndinati kwa woyang'anira, ine ndinati, "Kodi nyali izi ndi zotsimikizika kuti nzodalirika?"

"Zodalirika, ndendende."

"Izo sizikabwezedwa?"

"Ayi, bwana."

168 "Ndipo izo ndi zodalirika? Momwe zinapangidwira ndi chirichonse ndi zodalirika?"

"Inde."

169 Ine ndinawona iwo anapanga kuwala kofewa kokongola. Mkazi aliyense angayamikire izo mchipinda. Inu mukudziwa chimene ine ndinachita? Ine ndinangozitengera pafupifupi thuu handirede za izo, ndipo ine ndinayamba kuzungulira kwa aliyense amene ine ndinkamudziwa.

170 Anati, "Kodi iwe ukufuna chiyani, mmawa uno, Billy? Kodi sindinalipire bilu yanga?" Ine ndinkayenera kutolera mabilu.

171 Ine ndinati, "Oh, munalipira bilu yanu. Ine ndikufuna ndikupangireni inu ina." ine ndimati, "Ndiri ndi nyali apa."

"Oh, sindingayikwanitse iyo."

172 "Tsopano dikirani miniti. Sindinakufunseni inu kuti mugule. Ine ndangokhala nazo zochuluka chotero za izo, ine—ine ndikufuna kusiya imodzi m'nyumba mwanu. Inu mungoyisunga iyo masabata angapo, ndipo musangalale nayo, ndipo ine ndidzabwerera ndi kudzayitenga iyo. Ife tikuyenera

kulengezetsa zinthu izi, kungozitulutsa izo, kotero ndingoyika iyo mnyumba mwanu."

173 "Chabwino, tsopano, Billy, ine—ine sindingathe kugula iyo. Ndilibe ndalama zogulira iyo."

174 "Ine sindinakufunseninso kuti mugule iyo, sichoncho ine? Ndangonena kuti ndikungofuna kuyika iyo mnyumba mwanu, ndikuloleni kuti musangalale nayo."

"Palibe kuserewula?"

175 "Osati kachidutswa ka mbeza. Inu mumandidziwa ine. Ndidzabwera kudzayitenga. Ndidzayitenganso pakatha masabata awiri. Chabwino. Ndidzabwera ndi kudzayitenga iyo. Chinthu chokhacho chimene ine ndikufuna kuti inu muchite, ndicho basi. . .Ndikufuna kuyitsitsa mu galimoto yanga, ndipeze malo oti ndiyiyike iyo. Ndikuyenera kutsitsa zambiri za izo pano. Ine—ine—ine ndikufuna kuchotsa izo mu galimoto yanga. Ine—ine sindikufuna kuti inu mugule iyo. Sindinakufunseni kuti mugule iyo. Ndangokupemphani kuti mulole iyo ingokhala apa."

"Chabwino, bwanji ngati itasweka?"

"Umenewo ndi udindo wanga. Ine ndi amene ndayima kumbuyo kwake."

176 Ine ndinadziwa kuti nyaliyo idzigulitsa yokha. Ine ndinadziwa kuti iyo inali chipangizo chenicheni. Ndinayika nyaliyo m'nyumbayo. Sindinatenge teni mwa thuu handirede. Ndinapambana mpikisanowo. Chifukwa chiyani? Bwanji? Nyaliyo inadzigulitsa yokha. Inu mukayiona iyo, ndi kuona chomwe iyo ili, ndiye inu muyifuna iyo. Iyo idzigulitsa yokha.

177 Ndi chinthu chomwecho. Sitikuyenera kukhala ndi mabungwe aakulu kuti timugulitse Khristu. Sitikuyenera kukhala ndi alaliki ophunzira kwambiri, ndi anthu opukutidwa kwambiri omwe ali mameya, ndi zinthu zosiyanasiyana za mzinda. Chimene ife tikuyenera kukhala nacho ndi Khristu. Ndipo Khristu amadzigulitsa Yekha. Inu mukamuyika Khristu mu mtima wa munthu, simusowa kumuuza iye, "Ukuyenera kujowina bungwe *ili*, kapena *ilo*." Iye wagulitsidwa kale pa chinthucho.

178 Muli ndi njala? "Odala ndi iwo akumva njala ndi ludzu." Tikukonzekera kubwera pa gome la mgonero tsopano. Kwa iwo omwe sanayambebe, mwina, sanatengepo Khristu mmoyo wanu. . .Ngati inu muli Mkhristu, ndiye inu muli ndi njala. Ine ndakhala Mkhristu, zaka sarte-wani tsopano, ndipo tsiku lirilonse ndimamva njala ya Khristu kuposa momwe ndinkachitira pamene ndinkayamba. Iye amakomerakomera pamene masiku akupita.

179 Ndipo ine ndimayang'ana zikwangwani Zake zazing'ono, pamene ine ndiwona iwo akupita kumusi mu msewu, kuwawona

iwo kunja kuno mu chipatala, kuwawona iwo mu ora la imfa yawo, kuwawona iwo kunja kuno pamene iwo ali pa chiwonetsero, kumuwona dona wamng'ono uyo, momwe iye amadzigwirira yekha pamenepo monga woyera weniweni, weniweni.

180 Ine ndinayima pa kauntala, kuno osati kale kwambiri, ndinkamuyang'ana dona wamng'ono. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi.] . . . akuyamba, kutembenuka. Anati, "Kodi mumamudziwa Yesu ngati Mpulumutsi wanu?" Ndipo mnyamatayo anagwetsera mutu wake pansi, anathamangira kunja kwa chitseko, mwaona, sanayang'ane konse pa ine. Ndi zimenezotu. Oh, iye sankandidziwa ine, koma ine ndinkamudziwa iye. Ine ndinkamudziwa iye. Ndinkamuyang'ana iye. Iye anakwatiwa tsopano. Iye anakwatiwa ndi mlaliki wamng'ono, ndipo akungochita bwino.

181 Chotero ndi zimenezo, inu mwaona, ine ndimakonda kuona chikwangwani chimenecho. Ndimakonda kuwona icho. Icho—icho chimandipangitsa ine kukhala ndi njala, kufika pa malo pamene, uko, ife tikhoza kudya, kudya Chakudya chauzimu. Chifukwa, ine ndimadziwa kuti mtsikana ameneyo sanali wa mpingo. Iye anali Mkhristu. Uko nkulondola. Inde. Mutha kunena.

182 Baibulo linati, "Ngakhale Petro ndi Yohane . . ." (Atachiritsa mwamuna uja pa chipata chotchedwa Chokongola; anali wolumala kuchokera mmimba mwa amayi ake, mwaona, analibe mphamvu zambiri, samatha kuyimirira nthawi yayitali, Petro anachita kumugwira iye kuti ayambe kuyenda. Anachiritsidwa . . . Kuchokera mmimba ya amayi ake, mwaona. Pamene iwo anawatengera iwo ku bwalo ndi kuwaletsa iwo kuti azilalikira mu Dzina la Yesu.) "Ndipo iwo anazindikira kuti iwo anali mbuli," Baibulo linatero. Atumwi amenewa, Yohane ndi Petro, anali "anthu osadziwa ndi osaphunzira." Iwo sankadziwa zaumulungu zazikulu zirizonse. Iwo anali asodzi, sankatha kulemba dzina lawo. Koma anati, "Iwo ankayenera kuwadziwitsa iwo, kuti iwo anali ndi Yesu."

Kodi iwo anali chiyani? Zikwangwani, zikwangwani.

183 Oh, ife tikhoza kumapitirira. Mulungu atithandize ife kukhala zikwangwani. Mulole Branham Tabernacle uyu apa, malo aang'ono awa apatulidwe ndi kuperekedwa kwa Mulungu, mulole iwo atulutse zikwangwani zazing'ono kudutsa dziko lino, zimene zipangitse fuko lonse ili lanjala ndi laludzu kuti libwere kwa Khristu, lingakhale pemphero langa.

Tiyeni ife tiweramitse mitu yathu miniti yokha.

184 Atate wachisomo choposa, ife ndithudi ndi anthu amwayi kukhala ndi Khristu m'moyo mwathu ndi m'mitima mwathu. Ndife oyamikira kwambiri chifukwa cha Iye, Atate athu. Ife tikudziwa kuti kumudziwa Iye ndi Moyo. Osati kudziwa

tizikhulupiriro, osati kudziwa mabukhu, koma kudziwa Khristu ndi Moyo. Ndipo, Atate Mulungu, ife amene tamupeza Iye mwanjira imeneyo, Mpulumutsi wathu, Mchiritsi wathu (mphamvu yathu, thandizo lathu—thandizo lathu limachokera kwa Ambuye), tikuvomereza kuti ife tiri chabe; sitikudziwa kanthu. Pali chinthu chimodzi chokha chimene ife timachidziwa kapena tikufuna kuchidziwa: Ndicho Khristu mu mphamvu ya chiwukitsiro Chake. Pakuti aliyense amene akhulupirira iyo ali ndi Moyo Wamuyaya.

185 Ndipo ife tikupemphera, Atate Akumwamba, kuti Inu mudalitse mpingo waung'ono uwu ndi anthu awa amene ali pano pa usiku wotentha uwu, pa madzulo a Sabata awa kuno, atakhala mu kachisi wamng'ono uyu, wamatabwa, akuyembekezera madalitso a Mulungu.

186 Mawu ochepa osakanikirana ndi osweka amene aperekedwa: anjala, ndipo wapaulendo amaona chikwangwani. Mulungu, tipangitseni ife kukhala ndi njala ndi ludzu kuti ife tiziwona zikwangwani Zanu, kuwona miyoyo ya Chikhristu. Tiloleni ife tikhale zikwangwani Zanu. Muwonetsere Moyo Wanu kwa moyo wanjala, kuti iwo akhale ndi njala akawona chikwangwani chimene tikuchitsatira: "Khristu, Wotithandizira wathu, watipatsa ife moyo wamtendere wa chimwemwe chodzadza ndi mphamvu mmoyo wathu."

Ndi kukhala moyo kuti anthu afune kukhala monga Iye; perekani izi, Ambuye, perekani izi kwa ife tonse.

187 Ndipo mulole pakhale ena pano amene sanapezebe zimenezo; koma usikuuno iwo akhala akuphunzira, ndi kuyang'ana motsatira, kutsika kupyola mu ulendo wa moyo kupita kwa anthu oyera akale osiyanasiyana: amayi akale amenewo a masiku apitawo; munthu uja amene iwo ankamuseka pangodya ya msewu ndipo ankaganiza kuti iye anali . . . wosokonezeka maganizo, atayima kunja uko akulalikira. Koma tsopano akuwona kuti munthu ameneyo anali chikwangwani. Iye anali chizindikiro chimene chinkalozera. Mayi wokalamba woyeretsedwa uja amene anapita mu msewu tsitsi lake lopiringizika kumbuyo kwa mutu wake, atavala mwachikale, ndipo komabe, ife achinyamata mwina tinawaseka iwo ndi kuganiza, "Ndi mtundu wanji wa chosema umenewo?"

188 Koma ife tikuzindikira, Ambuye, icho chinali chikwangwani cha Moyo Wamuyaya. Ife tinachilambalala icho, Atate. Ife tikupepesa. Ife tikupepesa. Tiloleni ife tibwerere mmbuyo ndi kubwereza izo usikuuno, Atate. Tipangeni ife monga choncho. Tipatseni ife Moyo. Ife tikufuna kuti tiziwoneka ngati oyera pamaso Panu. Ife tikufuna kuti tizichita monga izo. Mwamuna uja amene ife tinkamuyankhula zoyipa, mwamuna uja amene ife tinakangana naye, sanayankhe kalikonse koma anali wokoma kwambiri. Iye anati, "Izo zonse ziri bwino,

mwana. Ambuye akudalitse iwe." Ndipo ife tinaseka pamaso pake ndipo tinachokapo. Oh, Mulungu, posadziwa kuti icho chinali chikwangwani, posadziwa kuti munthu ameneyo anali chikwangwani chotsatsa Moyo Wamuyaya kwa ife. Iye anali ndi Khristu mmoyo wake.

189 Tsopano, ife tiri ndi njala, Ambuye. Tikudziwa koti tipite. Ife tikufuna kuti tipite ku malo awa amene chizindikiro chikutilozera ife, ku Kalvare kumene ife tingapeze mtundu umenewo wa moyo. Kumene moyo wanjala ukhoza kukhutitsidwa. Eya, si mailosi atatu kumusi kwa msewu. Ndi sitepe imodzi yokha yowonjezera.

190 Mulungu, mupangeni wochimwa ameneyo, usikuuno, apange sitepe imodzi imeneyo: abwere ku Kalvare kuchoka ku matope ndi tchimo limene iye alimo. Mulole iye akokere pafupi ndi Kalvare pakali pano, ndi kuyima, ndi kuyang'ana mmwamba, ndi kuti, "Ambuye, ine ndachiwona chikwangwani Chanu, ndipo ndiri ndi njala. Dzazani moyo wanga wanjala." Perekani izi, Atate.

191 Pamene tiri ndi mitu yathu yoweramitsidwa, kodi pangakhale ena muno usikuuno amene akufuna kukokera pafupi ndi Kalvare ndi kunena, "Ambuye, dzazani moyo wanga wanjala, ndipangeni kukhala ngati Mkhristu weniweni, Akhristu a Baibulo, Akhristu amene ndimawawona lero, amene amakhalira moyo Mulungu"? Kodi mungafune kuti mukumbukiridwe mu pemphero? [Wina akuyankhula mu malirime ndi kutanthauzira—Mkonzi]. Kodi mungafune kukweza dzanja lanu tsopano, ndikuti, "Ndikumbukireni ine, M'bale Branham"? Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu. Mulungu akudalitseni inu.

192 Atate Akumwamba, pali manja ambiri akwezedwa. Ife tikukuthokozani Inu, pokumva Mzimu Wanu ukuyankhula kwa ife, kuwaitanira iwo ku gome la Ambuye. Oh, Mulungu, mulole iwo atenge sitepe Yamuyaya imeneyo pakali pano (osazabwerereranso), abwere ku Kalvare, mulole kuwala kwawo kuwale kuyambira tsopano, kuti ena awone ntchito zabwino, ndi kulemekeza Atate Kumwamba. Perekani izi, Ambuye. Ife tikuwapereka iwo kwa Inu tsopano, ngati zikho za chisomo, kupyolera mu Dzina la Yesu Khristu.

193 Pamene ife tikadali, ndi mitu yathu yoweramitsidwa tsopano, mphindi yokha. Onani ngati wina angafune kuti abwere kutsogolo, kupanga kuvomereza, kupemphera.

Iye asamala inu,
Iye asamala inu;
Mkuwala kapena mthunzi,
Iye asamala inu.

Iye asamala inu,

Iye asamala inu;
Mkuwala kapena mthunzi,
Iye asamala inu.

Tsopano ndi mitu yanu yoweramitsidwa, mulole Akhristu ayimbe.

Iye asamala inu,
Iye asamala inu;
Mkuwala kapena mthunzi,
Iye asamala inu.

Iye asamala inu,
Iye asamala inu;
Mkuwala kapena mthunzi,
Iye asamala inu.

194 Tangoganizani pamene dzuwa likuwala, Iye amasamala; pamene mithunzi igwa, Iye amasamala. Nanga bwanji mthunzi wa . . . chigwa cha mthunzi wa imfa? Iye adzakusamaliranibe inu. Kodi inu simusamala mokwanira za Iye usikuuno kuti muyende ndi kugwada pansi ndi gulu laling'ono ili pano tsopano? Pangani kuvomereza kwanu, kumuuza Iye kuti inu mukufuna kuti mubwere pafupi ndi Kalvare, tsopano.

Iye asamala inu.

Iye asamala inu,
Iye asamala inu;
Mkuwala kapena mthunzi,
Iye asamala inu.

195 Kutsika kupyola munjira pamene tikupita, mithunzi yakuya imagwa; koma Iye amasamala, Iye samachoka, ndipo samatitaya. Tsiku lina, pamene ife tidzafika kumapeto kwa msewu, ndi kuyamba ulendo wautali ndi wotsiriza umenewo, Ine ndikuyembekeza kuti Iye adzakhala kumeneko tsiku limenero. Iye adzakhalako. Inu muli ndi Wokuthandizirani usikuuno, Khristu akufuna kukuthandizani ngati mukufuna kuti kuwala kwanu kuwalire, kukhala chikwangwani cha Iye. Kodi inu simubwera, kukhala chikwangwani cha Khristu? Iye ndi Wothandizira wanu. Bwerani, mumutenge Iye tsopano pamene ife tikuyimba.

Iye asamala inu,

Pitani ku guwa ndipo mukapemphere tsopano.

. . . asamala inu; (Iye amasamala, inu mumasamala?)
Mkuwala kapena mthunzi,
Iye asamala inu. (Ngati Iye amasamala, kodi inu simusamala? Kodi inu simusamala, ngati Iye amasamala?)

Iye asamala inu,

Kazibwerani tsopano, mudzangogwada modekha, ndikuti, "Khristu, ine ndimasamala."

> . . . asamala inu;
> Mkuwala kapena mthunzi, (Nanga bwanji otopa ndi amanjenje ndi chirichonse okhumudwa?)
> Iye asamala inu.
>
> Iye asamala inu,
> Iye asamala . . . (Pamene dokotala abwera ndikuti, "Ziyembekezo zonse zapita.")
> Mkuwala kapena mthunzi,
> Iye amasamalabe . . .

196 Inu mukuti, "Koma, M'bale Branham, ine ndinachimwa motsutsa Mulungu."

> Iye asamala . . . (Inu mukuyenera kusamala. Iye amatero.)
> Iye asamala inu;
> Mkuwala kapena mthunzi,
> Iye asamala inu.

197 Mukuti, "M'bale Branham, ine ndiri ndi okondedwa. Ine ndachita *ichi*, *icho*."

Koma Iye amasamala. Iye amasamala chimodzimodzi basi.

"Ine ndakhala nazo zopweteka mtima zambiri, M'bale Branham. Ndiri ndi ana amene ali kunja mdziko. Ndiri ndi okondedwa amene . . . "

> Iye amasamala . . . (Iye amawona pemphero lirilonse, misozi iliyonse.)
> Iye . . . (Ine ndiri ndi ana awiri pa guwa usikuuno, chotero ine ndikudziwa Iye amandisamala ine.)
> Mkuwala kapena mthunzi,
> Iye asamala inu.
>
> Iye asamala . . .

198 Oh, Mulungu, momwe izo ziriri zoona. Inu mumatisamala ife, Ambuye. Ife sitikuyenera kusamalidwa, koma Inu mumasamala chimodzimodzi. Inu munasamala kwambiri mpaka Inu munapereka Moyo Wanu Womwe kuti ife tipulumutsidwe.

199 Azungulira guwa usikuuno ndi ana, a zaka zapakati, zaka zammatini, achikulire. Inu mumawasamala onse. Inu mumasamalira aang'ono. Mumasamalira a zaka zammatini. Mumasamalira okalamba ndi ofooka. Inu mumasamalira mayi wamng'ono, abambo aang'ono, amayi achikulire, abambo achikulire, mnyamata, mtsikana. Inu mumasamala. Inu mumasamala osasamalika, iwo amene sanasamale mmoyo, tawononga miyoyo yathu ndi moyo wachipwirikiti. Tachita

chirichonse chimene chiri cholakwika. Ife sitiri oyenera chisomo Chanu, Ambuye. Koma, Mulungu, ife tiri ndi njala.

200 Pozungulira ndi ena awa, Ambuye, payima awiri a ana anga, mwana wanga wamwamuna ndi wamkazi. Ine ndikuwapempherera iwo, Atate. Zikupangitsa mtima wanga kukondwera kuona iwo atagwada pansi apa, usikuuno, pamaso pa Mulungu wa bambo wawo. Ndikudziwa kuti Iye anandisunga ine mu zaka izi, Iye awasunga iwo. Anati, "Ndidzawasunga mu ora la kuyesedwa, limene likubwera ku dziko lonse." Inu mumatisamala, Ambuye.

201 Atsikana ndi anyamata ena agwada mozungulira apa. Mitima ya amayi ndi ya abambo ikukondwera. Mwinamwake amayi, abambo, ena pano, amene okondedwa awo anapita kwa zaka. Mayi wina wokalamba wopemphera mu Ulemerero, iye akuyang'ana pa chotchinga, usikuuno, cha Ulemelero, kutsika kupyola makonde Akumwamba. Iye akumuwona mwana wamkazi uyo, mwana wamwamuna uyo, akugwada pa guwa.

202 Inu mumasamala, Ambuye. Izo zikusonyeza Inu mumasamala.

203 Tsopano, uthenga waung'ono, kuti, "tikumva njala"; iwo akumva njala, Ambuye. Inu munanyezimiritsa Moyo Wanu mwa iwo. Iwo abwera kuno usikuuno kuti adzapatsidwe mphamvu, kapena kupangidwa chikwangwani cha Inu. Apatseni iwo Kuwala kwa dzuwa, Ambuye, mu mtima mwawo.

204 Mukhululukire tchimo lirilonse. Perekani izi, Ambuye. Iwo ndi Anu. Ndipo iwo ndi zikho za uthenga usikuuno, zoperekedwa kwa Khristu wamkulu amene anafa pa Kalvare. Mulole iwo abwere, Ambuye. Inu munati, "Chirichonse chimene inu mupempha, khulupiririrani kuti mwalandira chimene mwachipempha, ndipo mudzalandira icho."

205 Ine ndikupempha chipulumutso kwa moyo uliwonse pakali pano pa guwa ili. Ine ndikupempha, Ambuye, kuti iwo akakhale chikwangwani, kuyambira usiku uno mpakana; kuti m'moyo mwawo, moyo wawo wa tsiku ndi tsiku ukanyezimiritse Yesu Khristu, kuyambira wamng'ono mpaka wamkulu; kuti iwo sadzayiwala konse usiku uno; sadzayiwala nyimbo iyi, *Iye asamala Inu*; ndipo pamene iwo anali ndi njala ndi ludzu, Iye amasamala mokwanira kuti adyetse miyoyo yawo yotayika.

206 Khululukirani tchimo lawo, pakuti kwalembedwa: "Iye amene amva Mawu Anga, ndi kukhulupirira pa Iye amene ananditumа Ine, ali nawo Moyo wosatha. Iye amene adza kwa Ine sindidzamtaya konse kunja." Ndiye mosalabadira, Ambuye, za chikhalidwe cha moyo wawo, pamene iwo anabwera kuno, usikuuno, anagwada pa guwa ili, iwo anabwera kwa Inu, Ambuye. Ndi kosatheka kuti Inu musawalandire iwo, pakuti Mawu Anu sangalephere. "Ine sindidzataya konse. Iye amene

adza kwa ine, ndidzampatsa iye Moyo Wamuyaya, ndipo Ine ndidzamuwukitsa iye pa tsiku lotsiriza."

207 Ndi awa apa, Ambuye, akutenga Moyo Wamuyaya pakali pano, chifukwa Inu munati iwo adzakhala nawo, Moyo Wamuyaya, Moyo wa Mulungu Mwini mwa iwo, ndipo iwo sadzabwera ku chiweruzo. Koma ngati bomba la atomiki lingang'anime, iwo angapite kung'animako kusanachitike. Iwo adzakhala ndi Moyo Wamuyaya ndi kuukitsidwa, tsiku lotsiriza, kusandulika, kusinthidwa, kuchotsedwa mu dziko lino kupita ku Ulemelero. Iwo ndi Anu, Ambuye. Ine ndikuwapereka iwo kwa Inu ngati zikwangwani paulendo wamoyo.

208 Mulole atsikana aang'ono akhale chikwangwani mmasukulu, anyamata aang'ono akhale chikwangwani ku sukulu. Abambo ndi amayi, chikwangwani mu sitolo, kuntchito, mnyumba, mu dera. Apangeni iwo onse kukhala zikwangwani Zanu, pakuti iwo ndi Anu. Monga wantchito Wanu, ine ndikuwapereka iwo kwa Inu, mu Dzina la Yesu Khristu.

Iye asamala inu,
Tsopano, Iye . . .

209 Tsopano, kodi inu mumasamala za Iye? Kodi inu mukumufuna Iye ngati Mpulumutsi wanu ndi kukhulupirira kuti Iye amasunga Mawu Ake? Khulupirirani kuti Iye amasunga Mawu Ake; inu mubwere pa chikhulupiriro; khulupirirani kuti Iye amasunga Mawu Ake: "Iye amene adza kwa Ine, sindidzamutaya konse kunja."

210 Inu amene muti mumulandire Iye pa maziko achivundi, ndi kukhulupirira kuti chifukwa inu mwalapa, machimo anu akhululukidwa, inu mumulandira Iye ngati Mpulumutsi wanu, ndi kukhulupirira kuti Iye amakusamalani, ndikufuna inu kuti muyimirire, mutembenukire kwa anthu, kwa omvetsera awa ngati umboni kuti mumasamala za Iye, popeza Iye amasamala za inu. Kumbukirani, inu simukanabwera kuno pokhapokha ngati Iye akanasamala za inu. Tsopano, inu mumasamala za Iye, chotero inu muyime ndi kuchitira umboni, tsopano, kuti inu mumasamala za Iye. Kuyambira usiku uno, inu mukhala chikwangwani kwa Iye.

Iye asamala inu.

Iye . . . (Uko nkulondola, uko kulondola.) . . . inu,
Iye asamala . . .

Inu tsopano, amene mukukhulupirira kuti Iye amasamala za inu, ndipo inu mumasamala za Iye, imirirani pa mapazi anu, yang'anani mmbuyo kwa omvetsera kuti iwo awone. Iye anati, "Inu mukandivomereza Ine pamaso pa anthu, Ine ndidzakuvomerezani inu pamaso pa Atate."

Iye amasamalabe . . .

Inu mungokhala chiyimire pano, mphindi yokha, ngati inu mungathe.

Iye asamala inu,
Iye asamala inu;
Mkuwala kapena mthunzi,
Iye asamala inu.

Aliyense palimodzi tsopano.

Iye asamala . . . (Inu mukumukhulupirira Iye?)

[M'bale Branham akutumikira kwa amene ali paguwa, ndipo sakumveka bwino—Mkonzi.] . . . ? . . . Iye amasamala za inu? Chabwino, imirirani . . . ? . . .

211 Tsopano, omvetsera yang'anani kwacha a—anthu. Tsopano, tiyeni tonse . . . inu pano mwa omvetsera ingokwezani manja anu, ndi iwo mwa omvetsera, aloleni iwo akweze dzanja lanu, inu pa guwa, kwezani manja anu tsopano, pamene ife tikuyimba:

Iye asamala inu,
Iye asamala inu;
Mkuwala kapena mthunzi,
Iye asamala inu.

212 Tsopano, awa pa guwa, ine ndiyika mawu mkamwa mwanu, inu munene izi: "Yesu anandisamala ine. Ine ndinabwera kwa Iye, tsopano Iye amasamala za ine, ndipo ine ndimasamala za Iye. Kuyambira usiku uno, kuyambira pano, ine ndidzamutumikira Iye, ndipo ine ndidzakhala chikwangwani Chake kuyambira tsopano, Mulungu pokhala thandizo langa. Ameni."

213 Tsopano, lolani omvetsera tsopano ayime pa mapazi awo. Pamene anthu awa . . . Ndikufuna inu pano pa guwa kuti mugwirane chanza wina ndi mzake, ndikuti, "Mulungu akudalitseni inu, m'bale, mlongo," ndi, "Ine—ine ndikupemphera kuti inu mukhale chikwangwani cha Mulungu." Ndipo kenako akabwerera pa mpando wawo, inu mugwirane chanza nawo, kunena, "Mulungu akudalitse iwe, Myendamnjira. Iwe ndi mmodzi wa ife tsopano, ndipo ine ndidzikupempherera kuti ukhale chikwangwani."

214 Ndipo ngati anthu inu simunabatizidwe mu—mmadzi mu Dzina la Yesu Khristu, dziwe litsegulidwa mu kamphindi chabe. Chabwino.

Iye asamala . . . ? . . .
Iye asamala . . .

[M'bale Branham akutumikira kwa iwo ali paguwa—Mkonzi]. Oh, Mulungu . . . ? . . .

Oh, Iye amasamala inu,
Oh, Iye . . . (Atsikana aang'ono kuno pa guwa, akulira, agwirana wina ndi mzake manja awo.)

Monse kudutsa mkuwala kapena mthunzi,
Oh, Iye amasamala inu.

215 Tipatseni ife poyambira pang'ono tsopano, pa *Kuwala kwa dzuwa*. Iyi ndi ya atsikana ndi anyamata. Tiyeni tiyimbe iyo limodzi, ana aang'ono inu.

Kuwala kwa dzuwa, kuwala kwa dzuwa,
Yesu akufuna kuti ndikhale kuwala kwa dzuwa;
Kuwala kwa dzuwa, kuwala kwa dzuwa,
Ine ndikhala kuwala kwa dzuwa kwa Iye.

Tiyeni tonse tiyimbe iyo pamodzi.

Kuwala kwa dzuwa, kuwala kwadzuwa, (Lolani kuwala kwanu kuwale.)
Yesu akufuna kuti ndikhale kuwala kwa dzuwa;
Kuwala kwa dzuwa, kuwala kwa dzuwa,
Ine ndikhala kuwala kwa dzuwa kwa Iye.

Tiyeni tikweze dzanja lathu kwa Mulungu ndi kupanga lonjezo limenero kwa Iye.

Kuwala kwa dzuwa, kuwala kwa dzuwa,
Yesu akufuna kuti ndikhale kuwala kwa dzuwa;
Kuwala kwa dzuwa, kuwala kwa dzuwa,
Ine ndikhala kuwala kwa dzuwa kwa Iye.

216 Bwanji?

Iye asamala . . .

Tsopano, inu mugwirane chanza wina ndi mzake tsopano.

Iye . . . ( . . . ? . . . )
. . . mkuwala kapena mthunzi, (Muli ndi Lemba?)
Iye asamala inu.

Iye asamala inu,
Iye asamala inu;
Oh, mkuwala kapena mthunzi,
Iye asamala inu.

Tiyeni tikhale pansi tsopano, aliyense.

217 Atate Athu Akumwamba, ndi ora lachisomo mu chihema pamene titha kuwona miyoyo yambiri ikubwera ku guwa, ndi kukhetsa misozi ya—ya kulapa, ndi njala ndi ludzu la kwa Mulungu. Momwe ife tikukuthokozerani Inu chifukwa cha izi, ngakhale kukhudzika pa ana aang'ono, akuzeni iwo.

218 Mulungu pamene ife tikuyimba nyimbo zakuti *Iye Amasamala Inu*, ife tikudziwa izo, Ambuye. Ndi nyimbo ya ana aang'ono, *Kuwala Kwa Dzuwa*; "Kuwala kwa dzuwa, Yesu akufuna kuti ndikhale kuwala kwa dzuwa." Ndithudi, Iye

anati, "Mulole Kuwala kwanu kuwalire pamaso pa anthu, kuti iwo awone ntchito zanu zabwino." Atate, mulole izi zisakhale kwa aang'ono okha, koma mulole ife tonse tikhale monga ana aang'ono monga zinanenedwa kale, kuti, "pokhapokha ife titakhala ngati ana, sitingathe kulowamo; mitima yathu yaying'ono, yofewa, monga ana aang'ono, ife sitingawone Ufumu wa Mulungu."

219 Mulole mitima yathu ikhale ngati ana aang'ono. Ndipo ife tikufuna kuti tikhale mwanjira imeneyo, Ambuye, ophweka mmoyo wathu. Basi opanda kudzikweza, opanda chodzikuza, koma ophweka, ngati ana aang'ono, kukukondani Inu, ndi kukumverani Inu, ndi kukutumikirani Inu. Tikudziwa kuti sitiyang'ana nzeru za dziko ili, chifukwa ndi zopusa kwa Mulungu. Ife tikuyang'ana chifundo cha Mulungu ndipo ife tikupemphera kuti Inu mupereke chifundo kwa onse amene a—akufuna chifundo. Ndipo kwalembedwa: "Achifundo adzalandira chifundo."

220 Tsopano, ife tikuyandikira gome la Ambuye. Oh, ndi nthawi yoyenera bwanji, titawona ambiri. . .guwa litadzaza, akulapa: anyamata aang'ono, atsikana aang'ono, ana aang'ono, achikulire, a msinkhu wapakati, a zaka zammatini, abambo, amayi. Kuwawona iwo akubwera, akudzamulandira Yesu, akuyenda chapafupi ndi Kalvare chifukwa chakuti iwo akubwera ku gome la Ambuye.

221 Tsopano, mu zoyimira, Inu munatisiyira ife zoyimira ziwiri zokha: Chimodzi cha izo chinali Mgonero, chinacho chinali Kutsukanamapazi, ndi (zitatu, izo zinali), ndi Ubatizo, monga zoyimira: Mgonero, Kutsukanamapazi, Ubatizo. Zimenezo ndizo zoyimira, zakunja, zomwe ife timachita, zomwe zimayankhula za ntchito yamkati ya chisomo. Ife tikuyenera kumubatiza winawake mu mphindi zochepa mu Dzina la Yesu Khristu.

222 Atate, alipo ambiri pano akubwera ku gome la Ambuye. Mulole Mkhristu aliyense adziwe kuti Yesu ananena izi: "Iye amene adya thupi Langa, ndi kumwa Magazi Anga, ali nawo Moyo Wamuyaya; ndipo Ine ndidzamuwukitsa iye tsiku lomaliza." Ife tikudziwa Iye ananena izo. Tsopano, Atate, ife tikupemphera kuti Inu mukonzekeretse mitima yathu mu kukoma mtima ndi kulapa, kuti ife amene tikudza tisadzaweruzidwe pamodzi ndi dziko lapansi. Mulole ife tibwere monga Akhristu, pakuti ife tikupempha izi mu Dzina la Yesu. Ameni.

223 Pamene iwo a. . .othandizira, kapena, madikoni akubwera ndi gome la Ambuye, tiyimba nyimbo, *Pali Kasupe Wodzaza Ndi Magazi, Wotengedwa Kuchokera mu Mitsempha ya Emmanuele*, pamene ife tikukonzekera mgonero, mu kamphindi chabe, ndipo othandizira abwera, kapena, madikoni, ndi kubweretsa gome la mgonero pamene ife tikuyimba iyi.

Pali Kasupe wodzazidwa ndi Magazi,
Kuchokera mu mitsempha ya Emmanuele,
Ndipo ochimwa amadziponyera pansi pa kusefukirako,
Ataya mabanga a zolakwa zonse.
Ataya mabanga a zolakwa zonse,
Ataya mabanga awo onse. . .(Tangoganizani, mabanga a zolakwa zawo zonse.)
Ndipo ochimwa amadziponyera pansi pa kusefukirako,
Ataya kulakwa kwawo konse. . .

224 Tsopano, mwa kulemekeza, ife tiwerenga Mawu, opezeka mu mutu wa 11 wa Akorinto Woyamba, ndime ya 23. Paulo Woyera akuyankhula ku mpingo wa ku Korinto:

*Pakuti ndinalandira kwa Ambuye chimene* inenso *ndinapereka kwa inu, Kuti Ambuye Yesu usiku womwewo. . .umene anaperekedwa anatenga mkate:*

*Ndipo pamene anayamika, ananyema iwo, ndipo* iye *anati, Tengani,* ndipo *idyani: ili ndi thupi langa, lomwe* lina*nyemedwa chifukwa cha inu: ichi muzichita mchikumbutso cha ine.*

*Momwemonso* iye *anatenga chikho, ndipo pamene iye anadya, akuti, Ichi* ndi chikho *cha chipangano chatsopano mu magazi anga: ichi muzichita, nthawizonse* inu *mukamwa, mu chikumbukiro changa.*

*Pakuti* nthawizonse *pamene mudya mkate uwu, ndi kumwera chikho ichi,* inu *mukuwonetsera imfa ya Ambuye mpaka iye* adzabwere.

*Chifukwa chake aliyense amene adzadya mkate uwu, ndi kumwa chikho ichi cha Ambuye, mosayenera, adzakhala wolakwira thupi ndi magazi a Ambuye.*

*Koma munthu aliyense adziyese yekha, ndipo akatero iye adye mkate ndi kumwa chikho.*

*Pakuti iye amene adya ndi kumwa mosayenera, adya ndi kumwa chiwonongeko kwa iyemwini, posalizindikira thupi la Ambuye.*

*Pachifukwa ichi ambiri* adwala ndipo afooka *pakati panu,. . .ambiri agona.*

*Pakuti ngati ife. . .tidziweruza tokha, sitidzaweruzidwa.*

*Koma pamene ife taweruzidwa, ife timalangidwa ndi Ambuye, kuti tisadzudzulidwe limodzi ndi dziko lapansi.*

*Chifukwa chake, abale anga, pamene* inu *musonkhana kuti mudzadye, dikiriranani wina* ndi mzake.

225 Tsopano, mu kumvera kwa lamulo lalikulu ili, loperekedwa apa ndi Paulo Woyera, tiyeni ife tingokumbukira ichi: kuti ndife olakwa, kuti mwanjira ina ndi mwinamwake, opambana a ife ali olakwa pamaso pa Mulungu, chifukwa kwalembedwa za Ambuye Yesu Khristu wathu: "Chifukwa chake khalani angwiro, monga Atate anu Akumwamba ali angwiro." Chotero ife tikhoza kukhala angwiro kupyolera mu chikhulupiriro chathu mu magazi ake okhetsedwa. Pakuti palibe chinthu chimodzi chimene tingachite kuti tidzithandize tokha, tikuyenera kudalira mu chifundo Chake.

226 Chotero, ndikupemphererani inu kuti Mulungu akukhululukireni pa kusayenera kwanu konse. Ndipo kodi inu mundipempherera ine, kuti Mulungu andikhululukire ine chifukwa cha kusayenera kwanga? Pakuti ife tikuyandikira gome la Ambuye. Tipemphera, mwakachetechete, wina kwa mzake. [M'bale Branham ayima kwa theka la miniti—Mkonzi].

227 Perekani izi, Atate athu, mu Dzina la—la Yesu Khristu, Mwana Wanu. Ameni.

228 Kuyimira thupi la Yesu Khristu: mkate wopatulika uwu. Iye anatenga mkate ndipo anawunyema ndipo anapereka kwa ophunzira Ake ndipo ana-. . .anati, "Tengani inu ndipo idyani: ili ndi thupi Langa, limene lanyemedwera kwa inu: ichi muzichita mu chikumbukiro cha Ine."

229 Tiyeni tipemphere:

Atate Athu Amene muli Kumwamba, Dzina Lanu Liyeretsedwe. Ufumu Wanu udze. Kufuna Kwanu kuchitidwe pansi pano, monga ziliri Kumwamba. Mutipatse ife lero chakudya chathu chalero. Ndipo mutikhululukire ife zolakwa zathu, monga ife tiwakhululukira iwo amene atilakwira ife. Musatitengere ife kokatiyesa, koma mutipulumutse kwa woyipayo.

230 Oh, Ambuye Mulungu, Mlengi wakumwamba ndi dziko lapansi, Mwini wa Moyo Wosatha, ndi Wopereka mphatso yabwino iliyonse, yang'anani pansi pa ana a anthu ndipo khululukirani machimo athu, monga ife, mwa kulapa, tikugwada pamaso Panu, zolengedwa zosayenera ife tiri. Ndipo pamene tiona mtengo umene Mulungu analipira chifukwa cha machimo athu potumiza Mwana wake, wopangidwa muchifanizo cha thupi lauchimo, ndipo thupi Lake lamtengo wapatali, ndikuwona zipsyera za misomali m'manja Mwake, m'mapazi Ake, zipsyera za minga m'mutu Mwake, zopyoza pansi pa mtima Wake wamtengo wapatali. Zonsezi zinachitidwa chifukwa cha tchimo langa ndi machimo a anthu anga. Izi, Ambuye, tikulapa tchimo lathu.

231 Mkate uwu ukuyimira thupi lonyemedwa limene tikuyenera kulitenga pomukumbukira Iye. Oh, Atate Mulungu, yeretsani

mkate wopatulika uwu kwa cholinga chimenecho. Ife tikupempha mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni.

232 "Momwemonso Iye anatenga chikho, ndipo pamene Iye anadya, anati, 'Awa ndi Magazi, Chipangano Chatsopano: muzichita ichi mu chikumbutso cha Ine. Pakuti nthawizonse pamene inu mumwa, mukuwonetsera imfa ya Ambuye mpaka Iye adzabwere.'"

Mulungu Wamphamvuzonse, Mlengi wakumwamba ndi dziko lapansi, ndi Mwini wa Moyo wabwino, Moyo Wamuyaya, Moyo wokhawo, Atate Mulungu, ife tikupereka kwa Inu chipatso ichi cha mpesa. Chimene, ife tikukumbukira, mu mtima Wanu waukulu, wopatulika, wamtengo wapatali, monga Inu, usiku umenewo, munkadziwa kuti Inu munkawasiya okondedwa Anu, munawayitanira pambali, ndipo munadya mgonero, ndipo munati kwa iwo, "Ine sindidzamwanso chipatso cha mpesa, mpaka ndidzamwe a-. . .ndi inu kwatsopano mu wa Atate Anga Mmwa-. . .Ufumu." Ife tikuyembekezera tsiku limenero pamene ife tidzamwa ndi Inu mwatsopano mu Ufumu wa Mulungu. Usiku waukulu, wodziwika uja umene udzabwere pamene Mgonero wa Ukwati udzafalikira mu mlengalenga, ife tidzayima pamenepo owomboledwa ndi Magazi amene mpesa uwu ukuyimira.

233 Oh, Mulungu, yeretsani vinyo wopatulika uyu ku cholinga chake kuti ayimire Magazi a Ambuye wathu Yesu Khristu. Ndipo mulole aliyense amene atadye mkate uwu ndi vinyo, mulole iwo alandire mphamvu Yauzimu, thandizani, chiritsani matenda awo, khululukirani machimo awo, Ambuye. Chiritsani matenda anga ndipo mundikhululukire machimo anga. Ndipo tipangeni ife anthu Anu, antchito Anu, pakuti ife tikupempha izi, mu Dzina la Yesu Khristu. Ameni. [Malo opanda kanthu pa tepi—Mkonzi].

234 . . .mutsalire mpaka m'mawa.

> *. . .mgonero utatha, mdierekezi* tsopano *anayika mu mtima wa Yudasi Iskarioti, mwana wa Simoni, kuti amupereke Iye;*
>
> *Yesu podziwa kuti Atate anamupatsa zinthu zonse m'manja mwake,. . .kuti iye. . .anachokera kwa Mulungu, ndipo anapita kwa Mulungu;*
>
> *Iye* ananyamuka *pa mgonero, ndipo anavula* chovala *chake; ndipo anatenga chopukutira, ndipo anadzimanga m'chiuno.*
>
> *Pamapeto. . .iye* anathira *madzi mu beseni, ndipo anayamba kusambitsa mapazi a ophunzira, ndi kuwapukuta iwo ndi chopukutira chimene iye anadzimanga nacho.*

*Kenako iye anadza* kwa *Simoni Petro: ndipo Petro* anati *kwa iye, Ambuye, inu mundisambitsa mapazi anga?*

*Yesu* anayankha. . .*anati kwa iye, Chimene Ine ndichita* tsopano *iwe sukuchidziwa*. . .*; koma iwe* udza*dziwa mtsogolo mwake*.

*Petro* anati *kwa iye, Inu* simu*dzasambitsa mapazi anga konse. Yesu anamuyankha iye, Ngati Ine sindikusambitsa iwe, iwe sukhala ndi gawo ndi ine.*

*Simoni Petro* anati *kwa iye, Ambuye, osati mapazi anga okha, koma*. . .*manja anga ndi mutu wanga.*

*Yesu* anati kwa *iye, Iye amene wasambitsidwa alibe* kusowa *koma kusamba mapazi ake, koma* ndinu *oyera paliponse:*. . .*inu ndi oyera, koma si nonse.*

*Pakuti iye anadziwa amene adzamupereka Iye; chifukwa chake* iye anati*, Inu nonse si oyera nonse.*

*Chotero iye atatha kusambitsa mapazi awo, ndi kutenga* chovala chake, *ndipo*. . .*anakhalanso pansi, anati kwa iwo, Inu mukudziwa chimene ndachita* kwa *inu?*

Inu *mumanditcha ine Mphunzitsi ndi Ambuye: ndipo* inu *mumanena bwino; pakuti ndi chomwe ine ndiri.*

*Ngati Ine ndiye, Ambuye ndi Mphunzitsi wanu, ndakusambitsani mapazi anu;* inunso *mukuyenera kusambitsana mapazi wina ndi mzake.*

*Pakuti ndakupatsani inu chitsanzo, kuti* inu *muzichita monga Ine ndachita kwa inu.*

235 Kwa watsopano amene angakhale mu kachisi, uwu wakhala mwambo wathu chiyambireni ine kukhala mtumiki kuno, ndipo udzakhala mpaka masiku. . . masiku anga sadzakhalaponso. Ndi mwambo kuti pambuyo pa Kutsukanamapazi, ife. . . pambuyo pa Mgonero, timapanga Kutsukanamapazi. Ndikuganiza kuti ndi dongosolo lochokera kwa Ambuye. Azimayi amapita ku chipinda chimodzi ndipo amatsukana mapazi a wina ndi mzake, monga chitsanzo.

236 Panali zinthu zitatu zokha zimene Yesu anatisiyira kuti ife tizichita. Chimodzi (chimene chinali chachirengedwe), chimodzi cha izo chinali Ubatizo wa Mmadzi; chinacho, Mgonero; ndipo china chinali Kutsukanamapazi. Zinthu zina zonse, monga kugwira, kunyamula, ndi zina zotero, zinasiyidwa pa mtanda. Koma zinthu izi zinalamulidwa kuti zizichitidwa.

237 Ndipo ife tikupeza kuti zaka sarte-firii zitachitika izi, Paulo akulalikira, kapena, akumuuza Timoteo, kuti ngakhale mkazi wamasiye amene anali wosafika zaka sikisite sakanalowetsedwa mu gulu la okhulupirira, pokhapokha ngati anachereza alendo,

anapemphera kosalekeza usana ndi usiku, ndipo anasambitsa mapazi a oyera mtima. Kuwonetsera kuti Kutsukanamapazi kunkachitikabe patadutsa zaka zambiri. Ife tiri ndi umboni wa izo kudutsa mu mibadwo.

238 Ife timapangabe kuno monga njira yachikale ya Baibulo; izo ife timachita izi chifukwa ndi ulamuliro. Ndi lamulo lochokera kwa Ambuye kuti tizichita zinthu izi mpaka Iye adzabwerenso, kuwonetsera kuti ife timakhulupirira mwa Iye, kuti Iye anachita izo, ndipo Iye anati apa, "Ndakupatsani inu chitsanzo, kuti muzichita kwa wina ndi mzake monga Ine ndachitira kwa inu. Okondwa ndi inu ngati mukudziwa zinthu izi, ndi kuzichita izo." Kotero ndi kuti, chikhulupiriro chathu mu Baibulo, kuti tikuyenera kuchita, pambuyo Mgonero, Kutsukanamapazi. Ine ndikuganiza nthawi yomweyo motsatira izo ndi utumiki wa Ubatizo.

239 Ndikudziwa kuti nthawi yatha pang'ono, koma mukukumbukira tsiku limene abwana athu anatipempha ife kuti tigwire ntchito yowonjeza pang'ono kapena chinachake? Nanga bwanji kulambira Ambuye? Nthawi zambiri ankalalikira usiku wonse mu nthawi ya Baibulo. Ndikukumbukira nthawi ina mu Baibulo, powerenga pamene Paulo, akulalikira usiku wonse, mnyamata wina anagwa pazenera ndipo anafa. Paulo anapita ndipo anakangoyika thupi lake pa thupi la mnyamatayo, ndipo moyo unabwerera kwa iye kenanso, ndipo iye anakhala moyo. Ndipo uwu ukadali Uthenga womwewo, Uthenga wa Paulo, umene timalalikirabe, Uthenga wa Yesu Khristu.

240 Chotero tsopano, akazi ali ndi chipinda kumbuyo *kuno*, ndipo amuna ali ndi chipinda *kuno*. Ndipo tsopano, ngati inu mungatsalire ndipo kutha. . .mukufuna kuwonera msonkhano wa Ubatizo. . .Aliyense wa inu akufuna kubatizidwa, ife tiri ndi zovala pano zokonzekera msonkhano wa Ubatizo, umene ukhalepo zikangotha izi, umene utatenge pafupifupi, mwina, maminiti eyiti kapena teni kuti amalize uba-. . .msonkhano Wotsuka mapazi.

241 Ndipo ngati anthu inu, amuna kapena akazi, amene simunapangepo izi, ndipo mukufuna mdalitso mmoyo wanu, podziwa kuti mukuchita izo, basi, pamene mudzimangirira chopukutira kuti mugwade pa mapazi a m'bale wanu, kuti mutsuke mapazi, mungokumbukira kuti Yesu anadzikulunga chopukutira Iyemwini tsiku lina, ndipo anagwada kuti atsuke mapazi a msodzi. Ndipo Iye anati, "Ndikupatsani inu chitsanzo, kuti muzichita kwa wina ndi mzake monga Ine ndakuchitirani inu." Mungosunga izo mmalingaliro anu, ndipo ndikutsimikiza kuti pali mdalitso patsogolo panu. Mulungu akudalitseni inu, tsopano.

242 Aloleni akazi apite kuchipinda icho. Ndipo ngati mukungofuna kukhalabe pa msonkhano wa Ubatizo,

mungokhala pa mpando wanu, msonkhano wa Ubatizo ukhala ukutsatira msonkhano uwu pomwe pano. Ndipo amuna abwera kumbuyo *kuno*, ndipo akazi apita kumbuyo *uko*. Mulungu akudalitseni.

Uko nkulondola, Teddy, ungosiya nyimbo iziyimba.

61-0903 Mulole Kuwala Kwanu Kuwalire Pamaso Pa Anthu
Branham Tabernacle
Jeffersonville, Indiana U.S.A.

CHICHEWA

©2024 VGR, ALL RIGHTS RESERVED

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org

## Chidziwitso kwa ofuna kusindikiza

Maufulu onse ndi osungidwa. Bukhu ili mukhoza ku printa kunyumba kwanu ngati mutafuna kuti mugwiritse ntchito inuyo kapena kuti mukawapatse ena, ulere, ngati chida chofalitsira Uthenga wa Yesu Khristu. Bukhu ili simungathe kuligulitsa, kulichulukitsa kuti akhalepo ambiri, kuikidwa pa intaneti, kukaliika pakuti ena azitengapo, kumasuliridwa mu zinenero zina, kapena kugwiritsidwa ntchito ngati njira yopezera ndalama popanda chilolezo chochita kulembedwa ndi a Voice Of God Recordings®.

Ngati mukufuna kuti mumve zambiri kapena ngati mukufuna zipangizo zina zimene tiri nazo, chonde mulembere ku:

VOICE OF GOD RECORDINGS, MALAWI OFFICE
P.O. BOX 51453, LIMBE, MALAWI

VOICE OF GOD RECORDINGS
P.O. BOX 950, JEFFERSONVILLE, INDIANA 47131 U.S.A.
www.branham.org